


ISRAELI NDI MPINGO ²

 . . . nthawi ya—ya msonkhano uno, ife tikutsegula Baibulo tsopano ku mutu wa 1 wa Eksodo, kuti tiyambe usikuuno kuphunzira. Ndi phunziro lalitali, lalitali kwambiri, ndipo tikuyesetsa kulisanja ilo basi—mausiku angapo. Chifukwa chimene ine ndikuchitira izi, kuti ine ndikukhulupirira chitsitsimutso chizipitirira kudutsa Isitara, ndipo mwinamwake kumapitirirabe. Ife sitikufuna kuti tiyambe mochuluka za . . . pamene iwe ukungomverera njira yako. Ndine wokhulupirira wamkulu mu zimenezo.

² Ndi chifukwa chake ine ndiri pano mu chitsitsimutso ichi, ine—ine sindikudziwa. Ine . . . Izo zonse ndi chinsinsi kwa ine. Pamene manenjala anandiimbira ine madzulo ano za misonkhano uko ku Macon, Nashville ndi kudutsa kumeneko, ndipo ife talepheretsa chirichonse. Ena a iwo anali ndi nyumba zoyankhuliramo zomwe ife takhala tikuyesera kupeza kwa zaka zitatu kapena foro, faivi zapitazi, kukhala mpaka, ochuluka, anthu twente sauzande. Ndipo a . . . ife tinachoka pa msonkhano womaliza (mundikhulukire ine) ku Meridian, tinali nawo forte-faivi handiredi mkati, ndipo sitikudziwa amene anali kunjako, atayima mu mvula ndi mikuntho ndi zinthu, ife . . . ataimirira kunja uko. Ndipo pamene ife tinachoka ku Tallahassee, izo zinali chimodzimidzi, ife sitinakhoze ngakhale kuti tipeze malo oyikapo anthu. Ndipo Mzimu Woyera unati, “Ima. Kazipita kunyumba tsopano, kadikirire, ine ndikukonzekera kukutumiza iwe kutsidya kwa nyanja.” Chabwino, ndine ndiri pano.

³ Ine ndangolepheretsa misonkhano seveni. Ndangotsiriza kumene kulepheretsa misonkhano seveni, ndipo umodzi wa iwo kuno mu Indiana, Connerville. Ndipo umodzi wa iwo uko mu Alberta, Canada, pa bwalo lalikulu kumeneko, mumakhala anthu twente-faivi sauzande, ife takhala tikuyesetsa kuti tipeze bwalo limenelo kwakanthawi. Ndipo basi pamene ife talipeza ilo, ndipo chirichonse chakonzeka kuti tiyambitse msonkhano wa fuko lonse kumeneko kumene ife tikuyembekeza anthu sarte, forte sauzande, Mzimu Woyera unati, “Ima,” ndiyeno nkunditumiza ine kuno ku kachisi monga usikuuno. Mukuona? Mwaona, iwe umayenera kuchita zimene Iye akukuza iwe kuti uchite.

⁴ Inu mukuti, “Kodi inu mungasiye magulu a anthu ngati amenewo kuti abwere ku—ku kachisi wamng’ono kwambiri?” Chabwino, tsopano, dikirani miniti. Ife tikumutumikira Mulungu. Mukuona?

⁵ Filipo anasiya chitsitsimutso chachikulu, pamene iye

anali ndi Samariya yense akusunthika, ndipo anapita kutali mchipululu, Gaza. Ndipo anayima kumeneko kuti apeze munthu mmodzi, ndipo sanabwerere konse ku chitsitsimutsocho. Nkulondola uko? Mpaka ku chipululu, Gaza, anakapezako munthu mmodzi, wa chi Ethiopia, iye anatembenuzidwa. Ndiyeno iye anapotoloka kuchokera kumeneko, iye sanabwerere konse ku Samaria kachiwiri kumene iye anali ndi—chitsitsimutso chachikulu.

⁶ Tsopano, ife ndithudi tikuthokoza chifukwa cha utsogoleri wa Mzimu Woyera. Ife tiyenera kumapita momwe tikutsogoleredwa kuti tizipita. Ndipo ine ndamverera kutsogozedwa motsimikizika kwambiri kuti—kuti ndibwere kuno mu msonkhano uno kudzachita izi. Kodi ine ndangokhala pang’ono . . .

⁷ Oh, mundikhululukire ine, m’bale. Pano pali ena angapo, nawonso, M’bale Fleeman, ngati inu mungathe. Mwinamwake atengeni iwo, winawake yemwe alibe Baibulo. Chipangano Chakale, ife tikuphunzira mu Chipangano Chakale, makamaka, usikuuno, chifukwa ife tikutenga ndondomekoyo. Kwezani mmwamba manja anu, inu amene mungafune limodzi, koteri kuti iwo akhoze kulibweretsa ilo kwa inu. Muzibweretsa Mabaibulo anu, mapensulo anu ndi mapepala, ndi chirichonse, ndipo kuti muzikhoza kumalembapo mutuwo.

⁸ Usiku wathawu ife tinakhala mochedwerapo pang’ono, usiku wathawu. Ine ndiyesera mwakukhoza kwanga kuti ndiwombole zimenezo usikuuno, ngati nkotheke. Ine ndimangowakonda Mawu mwabwino kwambiri mpaka, pamene ine ndilowa mu Iwo, ine ndimangosocheramo. Ine ndikuganiza ife tinapita kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso usiku wathawu, njira yonse kudutsamo. Ine basi ndinangoiwala za nthawi yonse ndi china chirichonse.

⁹ Ino ndi nthawi yoyamba kuti ndikhale nawo umodzi wa misonkhano iyi, kwa zaka seveni, sabata yotsatirayi, ine ndinatseka chitsitsimutso ku kachisi. Ndi angati akukumbukira chomwe ulaliki wanga wotsanzikana unali? *Kodi Mfilisiti Wosadulidwa Uyu Ndi Ndani Akuyesera Kunyozza Ankhondo A Mulungu Wamoyo?* Umenewo unali ulaliki wanga wotsanzikana ku kachisi, zaka seveni zapitazo, wotsiriza, sabata ikubwerayi. Chabwino, mtsikana wanga wamng’ono apo anali usinkhu wa masabata awiri akubadwa. Ine ndinamulonjeza Mulungu ngati Iye “angandilole ine ndikhale kufikira iye atabadwa, ndiye ine ndidzapita.” Ndiyeno ine ndayenda kuyambira pamenepo, usiku kapena uwiri, uku ndi uko. Chotero, Ambuye anataliditsa ife mu njira zopambana. Penapake pafupifupi theka la milioni miyoyo yatembenuka mu wathu—msonkhano wathu womwe. Tangolingalirani za zimenezo, mu zaka seveni! Izo zikusonyeza. Sarte sauzande, mu tsiku limodzi. Inu mukudziwa, izo nzopambana. Nthawizonse ine ndikaganiza za zimenezo,

ndimapukusa mutu wanga. Lero, kulandira makalata ochokera uko ku Africa, amene anati, “Kummwera konse kwa Africa kwakondowezekanso, akonzeka,” tikungofuna kudziwa tsiku limene ife titi tidzabwerereko. Oh, mai!

¹⁰ Ndiyeno Ambuye anapereka masomphenya, ndipo anati, “Ku India, anthu firii handiredi sauzande amenewo akakhala pa msonkhano umodzi.” Inu zilembani zimenezo, mudzawone ngati izo ziri zoonza kapena ayi.

¹¹ Tsopano, zochuluka kwambiri pa zimenezo, zimene zimapitirira pa machiritso, zokhudza machiritso. Ine ndikuyesetsa kupeputsa malingaliro anga kwa zimenezo tsopano, kuti ndizingophunzitsa Mawu. Tsopano, ndine dzanja losauka pa zimenezo, koma ine—ine ndimakonda kunena zimene ine ndikuzidziwa za Iwo.

¹² Ndipo tsopano Lamlungu ife tidzakhala ndi, Lamlungu mmawa, mafunso, funso lililonse pa Lemba limene inu mukufuna lingaliro langa lake. Ndipo chotero ife tidzayesetsa kuzibweretsa izo kudutsa mu Baibulo mopambana momwe ife tingathere, Lamlungu mmawa. Inu muzibweretsa izo Lamlungu mmawa lisanafike, mpaka Loweruka usiku, funso lililonse pa Lemba, chirichonse chimene chimasokoneza malingaliro anu. Ndipo awo adzakhala mafunso, Lamlungu mmawa. Inu mukuzikonda zimenezo? Tsopano, ngati inu muli ndi chinachake, inu mudzangoti, “Ine sindikumvetsa momwe zinthu izi zingakhoze kukhalira.” Chabwino, mudzazibweretse izo ndipo tidzawone ngati tingapite limodzi, mwinamwake tonse a ife limodzi tikhoza kuzipeza izo. Ine ndidzachita mwakukhoza kwanga kwambiri kuti ndidzazifoletse izo mu Lemba, chifukwa ine ndikukhulupirira kuti izo ziyenera kukhala Mwamalemba kapena izo siziri zovomerezeka.

¹³ Tsopano, usiku wathawu ife tinatenga chiyambi choyamba cha “mpingo.” Mulungu akumulonjeza ndani? Abrahamu, amene ali atate wa ife tonse. Pakuti anali Abrahamu, lonjezolo linapangidwira; ndipo Abrahamu yekha amene anapangidwira lonjezolo, kwa iye ndi Mbewu yake. Ndi kulondola uko? “Abrahamu, ndi koma Mbewu yake.” Ndipo Mbewu yake sanali ana ake onse, koma, “Mwa Isaki Mbewu yake inaitanidwa.” Ndi kulondola uko? Ndipo apa pali zotsatira za Mbewu ya Abrahamu: Yesu Khristu ndiye Mbewu ya Abrahamu, ndipo ife, pokhala akufa mwa Khristu, timatenga Mbewu ya Abrahamu ndipo ndife olandira cholowa monga mwa lonjezo. Amen. Mulungu adalitsidwe!

¹⁴ Ife pano amene tikupitirira kuti tidutse, pamene mwamuna, mkazi adutsa zaka twente-faivi zakubadwa, inu mukhoza kukumana nazo izo, mwaona, masiku aunyamata anu atha. Ndipo kuganiza, lonjezo laulemelo limenelo, pamene ife tikuyang’anizana ndi kulowa kwa dzuwa. Ndi chiyani

chimenecho? Kodi moyo watha? Oh, ayi. Moyo sunayambe apobe. Oh, ife tikungopita! Ine ndikungolalakala pakanakhala njira ina imene ife tingakhoze kukhazikika, kufikira pakuti nthawi nkusatanthauza kanthu, ndi kungokhala muno monga chomwecho ndi kuzitulutsa zinthu zimenezo kuchokera m'Malemba, pamaso pa anthu. Iwo ali pamenepo, abwenzi. Ine ndikhoza kutsimikizira izo mwa Baibulo la Mulungu, ndi mothandizidwa ndi Mzimu Woyera, kuti mmodzi aliyense wa inu amene ali mwa Khristu, wobadwa mwatsopano, kuti limodzi la masiku awa imvi izo zidzasintha, ndipo makwinya adzachoka pa nkhope yanu. Inu mudzabwerera kukakhala mnyamata kapena mtsikana kachiwiri, ndikukhala ndi moyo kwanthawizonse ndi Khristu Yesu. Ine ndikhoza kukusonyezani inu pamene Mulungu anatsimikizira izo mu Baibulo, anasonyeza mithunzi ndi zilemba za izo, ndipo analonjeza izo ndi kulumbirira pa izo, kuti Iye adzazichita izo. Ndi zopambana bwanji! Ndidzamukonda mkazi wanga ndiye? Zedi, kuposa momwe ine ndikuchitira tsopano, ndithudi. Ine sindikudziwa momwe izo zidzakhalire, koma ine ndidzatero. Kodi iye adzakhala wanga? Zedi, adzakhala mzanga. Iye adzatero... osakhala ndi ana kapena kanthu, koma ana omwe ife tiri nawo kuno pa dziko lapansi adzakhala kumeneko ndi ife ngati iwo abadwa mwatsopano. Uko nkulondola. Kodi zimenezo sizikhala zopambana?

¹⁵ Ine ndinkakonda kuganiza, Amayi anakakonda kumandiuza ine (mundikhululukire ine, Amayi, izi zinali musanadziwe bwinoko, inunso) kuti ife tidzakakhala ndi mapiko ndi kumakawuluka tikuyendayenda kumeneko, inu mukudziwa. Ndipo, bwanji, ine ndimakonda kudya, kumwa, kugwirana chanza ndi anthu, chiyanjano. Ine ndinaganiza, "Oh, mai, zimenezo zikhala zitatha ndiye." Oh, ayi. Ine ndinadzapeza kuti Mulungu sanandipange konse ine Mngelo, Iye anandipanga ine munthu, ndipo ine nthawizonse ndidzakhala ndiri munthu ndipo sindidzakhala konse Mngelo. Kumeneko ndi kulakwitsa. Mulungu ali nawo Angelo, ndithudi, Iye anawapanga Angelo. Ndipo Iye anawapanga Akerubi ndi mapiko, ndipo Iye anawapanga Angelo opanda mapiko.

¹⁶ Pamene ine ndinkakonda kumva nyimbo zakale izi, pamene ine ndinali wochimwa ndi kupita mmalo amenewo, za "Mngelo wa maso a bulauni akundiyeembekezero;" Ine ndinkaganiza, "Oh, mai, Mngelo!" Ndipo ine ndinadzapeza kuti limenelo ndi bodza la mdierekezi. Kunalibeko chinthu choterocho. Mukuona?

¹⁷ Ndife amuna ndi akazi mwamtheradi. Ndipo ife tidzabwerera ku dziko lino, amuna ndi akazi. Uko nkulondola. Ndiko kuphunzitsa kwa Mulungu. Pamene uziwona zinthu zimenezo, izo zimakupangitsa iwe kumuyamikira Yesu Khristu.

¹⁸ Tsopano chimene ife tikuyesetsa kuti tichite usikuuno ndi kuponyera mthunzi, wa chimene Chipangano Chakale chinali,

ku Chipangano Chatsopano. “Ndipo zinthu zakale zonse,” Lemba limati, “zinali choyimira kapena mthunzi wa zinthu zomwe ziri nkudza.” Tsopano, phunziro lokongola usikuuno, Eksodo. Ife tinawasiya ana a Israeli usiku watha . . .

¹⁹ Kodi Israeli ankatchedwa chiyani iye asanakhale dzina lake Israeli? Ndani mu kalasi muno angakhoze kuyankha, kodi Israeli anali ndani iye asanapereke, asanapatsidwe dzina lauzimu limenelo? Tsopano, winawake asakhale mlaliki, ine ndinamuwona mlaliki akukweza dzanja lake mmwamba. Chabwino, winawake asakhale mmodzi wa alaliki inu. [Wina akuti, “Yakobo”—Mkonzi]. Yakobo, uko nkulondola. Ndipo chiyani—ndi chiyani chinamupangitsa iye kuti alandire dzina lauzimu limeneli? Winawake ananena chinachake. [M’bale akuti, “Anapambana ndi Mngelo.”] Anapambana ndi Mngelo, ndipo analimbana naye, ndipo anati, “Ine sindikulolani inu mupite kufikira mutandidalitsa ine.”

²⁰ Hei, inu mukufuna dzina lauzimu usikuuno? Ingogwirani Mzimu Woyera, ndikuti, “Ambuye, ine sindichoka pa kachisi uyu mpaka Inu mutandidalitsa ine,” zinthu zidzawoneka mosinthika pamene inu muzichoka. Inu mukhale otsimikiza basi monga Yakobo anachitira, inu mupeza mdalitso.

²¹ Ndipo, penyani, iye anakhudza ntchafu yake, ndipo Yakobo anayenda mosinthika. Ameni. Ine ndikuyembekeza zimenezo zikupita pansi mkati. Pamene iwe ulimbana ndi Mulungu, iwe umayenda mosinthika pambuyo pake. Penyani! Wamphamvu . . . Kumbali inayo ya mtsinje, mtsinje wawung’ono, iye anali munthu wamphamvu, wamkulu; wobwerera mmbuyo, chonchobe, kutali ndi Mulungu, akumuthawa m’bale wake, akuthawa kwa Mulungu; koma wojintcha ndi wamphamvu. Ndipo kumbali inayo ya mtsinje, kalonga wotsimphina. “Ndiwe kalonga pamaso pa Mulungu, chifukwa uli ndi mphamvu ndi Mulungu, ngati kalonga.” Kalonga wotsimphina, ndipo iye anatsimphina moyo wake wonse. Momwe Mulungu amachitira zinthu! Kodi Iye si wodabwitsa?

²² Tsopano, mbadwa, ife tinasiyira usiku wathawu, mu Genesis, pamene kuti wotsiriza wa foro amene Mulungu anapereka lonjezo Lake, anali Abrahamu, Isaki, Yakobo, Yosefe. Mulungu . . . Chinali chiyani icho? Mwa Abrahamu ife tinapeza, usiku wathawu, kwa mpingo wa Chikhristu lero, kusankhidwa, kusankhidwa. Ndipo mwa Isaki, kulungamitsidwa. Ndipo mwa Yakobo, chisomo.

²³ Inu muyenera kukhulupirira mu chisomo ngati mutawerenga moyo wa Yakobo. Inu muyenera kuwona kuti kunali kusankhidwa ndi kuyitana, chifukwa, oh, zinthu zimene munthu ameneyo anachita! Koma, komabe, Mulungu anali atamudalitsa iye. Mulungu anali atamuza iye zimene zikanati zidzachitike, chotero Iye anamuitana iye. Koma inu

mukuzindikira iye atatha kulimbana ndi Mngelo uyu, zinthu zinayamba kuwoneka mosinthika. Ndiye pamene iye anafika pamaso pa Farao, iye anati, “Umwendamnjira wanga wakhala zaka *zambiri*.” Mulungu anali atamudziwitsa iye kuti iye anali mwendamnjira.

Tsopano, ndipo mwa Yosefe, ungiwiro.

²⁴ Zindikirani, masiteji atatu. Kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro, kuyeretsedwa kupyolera mu Magazi, ubatizo wa Mzimu Woyera. Kenako ungiwiro, kupatsidwa ulemelero. Baibulo linati, “Iwo amene Iye anawalungamitsa,” izi ndi za kwa malingaliro auzimu, “Iye analandiranso ulemelero.” Ndi kulondola uko? “Iye amene Iye anamulungamitsa.” Ndiye ngati Iye watilungamitsa ife tsopano, ife tapatsidwa kale ulemelero mu chikhalidwe Chake. Osati Iye—Iye “*adzatero*.” Iye “*watero*” watipatsa ulemelero! Ndikuti, izo ndi zakuya, sichoncho izo? Koma ndi zimene Lemba limanena.

²⁵ Mulungu anamuuzwa Abrahamu, “Ine ndakudalitsa iwe, ndipo Ine ndakupanga iwe atate.” Osati “Ine ndidza.” “Ine ndatero! Ine ndakupanga iwe. Ndipo iwe udzabwera kwa Ine mu usinkhu waukalamba. Iwe udzapulumutsidwa. Ndipo Ine ndachita kale izo, Ine ndanena kale chomwecho. Iwe ulibe chochita nazo izo, izo ndi zopanda mangawa.” Mulungu anatsimikiza kuti adzakhala nawo mpingo Wake. Chotero nthawi iliyonse pamene Iye anapanga pangano ndi munthu, munthu amaswa pangano lake, ndipo iye akuchitabe koma. Munthu nthawi zonse amaswa pangano lake ndi Mulungu, koma Mulungu sangaswe pangano lake ndi munthu. Chotero, “Ine ndidza!”

²⁶ Inu mukuzindikira kumbuyo uko pamene Iye anamuuzwa Adamu pachiyambi, Iye anati, “Tsopano, musachite *izi*, ndipo inu mukhoza kuchita *izi*, ndipo musachite *izo*,” Adamu anapotoloka pamenepo ndipo anakaswa ilo. Koma ndiye Mulungu anawona kuti iye anali atatayika, Iye anati, “Ine ndidzaika udani, Ine ndidzaika udani pakati pa Mbewu yako ndi mbewu ya serpenti. Ndipo Iye adzavulaza mutu, ndipo, kapena Iye adzavulaza, wake—mutu wake udzavulaza Chidendene chako.”

²⁷ Tsopano, “Ine ndidza,” pamene Mulungu anena kuti Iye adzachita chirichonse, inu mukhoza kuyembekezera kuti icho chichitidwa. Pamene munthu anena kuti iye achita chirichonse, ine sindimadziwa za zimenezo. Koma Mulungu anamuuzwa Abrahamu kuti, “Ine ndidzakupulumutsa iwe, ndi Mbewu yako ya pambuyo pako.” Osati Abrahamu yekha, komanso Mbewu yonse ya Abrahamu. Mopanda mangawa! Ndikuti, ngati mungandikhululukire ine, ine ndikukhulupirira ine ndikhoza kufuula pang’ono. Taonani! Oh, inu simukuzindikira basi, anthu, chomwe izo zikutanthauza. Mwinamwake ena a

inu simunaganizirepo mozama mokwanira kuti mulowe mu zimenezo.

²⁸ Mulungu wawupatsa kale ulemelero Mpingo Wake. Iwo amene Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsanso ulemelero mu Mpingo, mwa Khristu. Ngati inu mwalungamitsidwa mwa Khristu, inu mwapatsidwa ulemelero mwa Khristu, kale, monga momwe Mulungu akukhuzidwira.

²⁹ Yesu anati, “Chotero khalani inu angwiro, ngakhale monga Atate anu Kumwamba ali wangwiro.” Inu mungakhale bwanji wangwiro? Koma pamaso pa Khristu, usikuuno, Mkhristu aliyense wobadwa kachiwiri ndi wangwiro. Ndine wangwiro basi mwa Mulungu monga Khristu anali, inu muli, inunso, wokhulupirira wina aliyense. Pakuti, si chiyero changa, ndi chiyero Chake. Mulungu sangavomereze changa, ine ndiribe chirichonse. Koma ine ndinabwera mwa Khristu, mwa chikhulupiriro. Ndipo, mwa Khristu, ine ndiri mwa Iye, ndi wangwiro pamaso pa Mulungu.

³⁰ Penyani! “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, ndipo timadzakhala ziwalo za Thupi ili.” Mu Aroma 8:1 “Chotero palibe kutsutsidwa tsopano kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu, amene sayenda monga mwa thupi, koma Mzimu.” Ndipo munthu yemwe ali mwa Khristu Yesu, amatsatira zinthu zauzimu. Kwa dziko, ndi malingaliro achithupi, izo ndi zopusa. Koma kwa iwo amene amakhulupirira, iwo ndi Moyo wosatha. Amen. Ndi zimenezotu. Oh, ndi zopambana bwanji! Ndiye nchiyani chingakupwetekeni? Inu muli mwa Khristu! Ndipo motsimikiza basi monga Mulungu anamuwukitsa Yesu kwa akufa, ife tidzabwera mwa Khristu. Amen. Inde, ife tiyenera kutero, Mulungu analonjeza kale izo. Pakuti, motsimikiza basi monga Thupi limenelo likukwera mmwamba ine ndiri mmenemo, Thupi limenelo, ine ndiyenera kupita nalo Ilo.

³¹ Tsopano mukuti, “Inu mumakhulupirira mu chitetezero Chamuyaya, ndiye, M’bale Branham?” Mwa njira ina, ine ndimatero. Ine ndimakhulupirira kuti Mpingo uli wotetezedwa Mwamuyaya, Mpingo uli. Mulungu ananena kale kuti iwo udzakawonekera pamaso pa Iye, wopanda banga kapena khwinya, Mpingo udzatero. Tsopano, chinthu chotsatira, ngati inu muli mu Mpingo, ndiye inu mumakhala otetezedwa ngati muli mu Mpingo.

³² “Iye amene abwera kwa Ine, Ine mwanjira iliyonse sindidzamtayira kunja.” Ndi kulondola uko? Ndipo mveterani, apa pali Mawu a Munthu a zimenezo, Yesu Khristu, Yohane Woyera 5:24, “Iye,” aliyenseyo, “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo (tensi yatsopano) Moyo wosatha.” Zimenezo si kungochokera ku msonkhano umodzi kupita ku wina. Moyo Wosatha! “Ndipo

sadzabwera ku chiweruzo” kapena chitsutso, sadzatayidwa konse, “koma wa (tensi yakale) wadutsa wachoka ku imfa wapita ku Moyo.” Yohane Woyera 5:24, Yesu ananena chomwecho. “Ine ndine Mkate wa Moyo umene umachokera kwa Mulungu Kumwamba. Makolo anu anadya mana mu chipululu, ndipo anafa, koma iye amene adya thupi Langa ndi kumwa Magazi Anga ali nawo Moyo wosatha, ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye pa masiku otsiriza.” Ndicho chimene Iye ananena.

³³ Tsopano, alipo ambiri amene amanyengezera kuti ali mmenemo. Alipo ambiri amene akudzimenyera okha nkondo, ndi kuyesetsa kuti azikhala moyenera ndi kuyesetsa kuti azikakamizira mkati. Ine sindikuzidziwa zimenezo. Koma ngati iwo ali mmenemo, izo zimangokhala zophweka basi kukhala moyo wa Chikhristu monga zimakhallira kukhala moyo uliwonse, chifukwa iwe uli mwa Khristu, ndipo palibe china koma kudzazidwa kokha ndi Mzimu Woyera kumakutsogolera iwe, ndi kukulondolera iwe ndi kukutsogolera iwe. Ndipo, bwanji, ndithudi inu mudzalakwitsa ndi kugwa, koma inu simungakhoze kukhala pansu, chifukwa, chimodzimodzinso momwe simungapangire a—phesi la chimanga a—kukhala mtengo wa mkuyu. Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Yesu anati, “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Inu muli nawo Moyo wosatha.

³⁴ Limodzi mwa matemberero aakulu pa mpingo masiku ano ndi mantha. Aliyense amawopa pafupi kufa, nde “Chichitike ndi chiyani, ndani, chiyani?”

³⁵ Bwanji, Yesu anati, “Ngakhale zowoneka zowopsya zikadzafika, dzakwezere ni mutu wanu ndi kusangalala, pakuti, chachikulu, chiwombolo chanu chayandikira pamene zinthu izi zidzachitika.”

³⁶ Tsopano, momwe Iye anawutengera Mpingo kudutsa mu ulendo umenewo! Momwe kumbuyo uko, ngakhale mwa Abrahamu ndi Isaki ndi Yakobo, ndi onse amenewo, tayang’anani pa zolakwitsa zomwe iwo anali nazo, koma Mulungu anali ndi iwo. Mthunzi. Tayang’anani pa Abrahamu kwa miniti.

³⁷ Ine—ine—ine ndikudziwa kuti ndiri nawo omvetsera a Arminian ambiri usikuuno, koma ine—ine ndikufuna ine—ine ndikufuna ndilongosole izi, kwa inu.

³⁸ Mulungu anamuuzza Abrahamu, mwa kusankhidwa ndi mwa chisomo, kuti, “Ine ndidzakubweretsa iwe kwa Ine, mu usinkhu wa ukalamba.” Mwakuyankhula kwina, “Ine ndidzakupulumutsa iwe. Ine ndidzakutenga iwe ndikudzakudutsitsa. Iwe udzakhala moyo wa nthawi yaitali. Iwe udzakhala ndi mwana. Osati... Pokhala opanda mwana, Sarah; iwe udzapita, ndipo iwe udzakhala ndi mwana. Ndipo, mwa mwana ameneyo, Ine ndidzapulumutsa naye dziko

lapansi.” Tsopano, Abrahamu asanachite chinthu chimodzi choti chimuyenereze icho, koma Iye mophweka basi . . . Mulungu anamuyitana iye. Izo zinali zonse.

³⁹ Iye anali basi Mkaldia kumusi uko mu mzinda wa Uri, anadzabwera uko mu zigwa za Shinara, kuchokera ku nsanja ya Babulo, kuchokera ku kupembedza mafano. Ine ndikuganiza abambo ake anali opembedza-mafano. Ndipo ine ndikuganiza Labani, atatha kufika kumusi uko, anatsimikizira izo, iye anali nawo mafano amenewo. Kodi iye akanawatenga kuti iwo, ngati iye sanabwere kuchokera mu nsanja ya Babulo? Ndipo kuchokera mwa anthu a Hamu kunabwera Nimrodi. Nimrodi anakhazikitsa nsanja ya Babulo, yemwe inali kupembedza-mafano, kupembedza-mafano koyamba pa dziko lapansi.

⁴⁰ Tsopano, ndipo penyani nsanja ya Babulo ija ikubwera mpaka mmusi, Babulo, ndi kumapitirira mpaka mmusi kudutsa kumeneko ndi kudzathera cha kuno mu Chivumbulutso; Mkhristu, kupembedza mafano kwachipembedzo, kumanamizira kukhala Chikhristu. Oh! Yohane anamuwona iye mu Chivumbulutso 17, anamusirira iye, momwe iye anakhalira, ankawonekera ngati, ndipo anavala Dzina la Yesu ndi china chirichonse, ndipo komabe ankawazunza ndi kupha ojera a Mulungu wamoyo. Mngelo anati, “Bwera kuno, ndipo ine ndikuwonetsa iwe yemwe iye ali.” Anati, “Iye ndi mpingo wawukulu umene ukukhala pamwamba pa ambiri, pa mapiri seveni, ndipo ukulamulira pa dziko lapansi, ndi zina zotero. Momwe iye anamwera magazi a ofera chikhulupiriro cha Khristu!” Oh, chifundo!

⁴¹ Anthu, ife tikukhala mu nthawi yotsiriza. Ndi angati a inu anthu omwe munamvapo zaka zapitazo kumusi kuno pamene iwo amati andimange ine kuno chifukwa cholalikira pa “chilemba cha chirombocho”? Pamene ine ndinanena kuti Mussolini, pamene iye anabwera koyamba mu ulamuliro zaka twente-zina-zosamvetsetseka zapitazo, ine ndinati, “Ngati Mussolini adzapite konse cha ku Ethiopia, mulembe izi, sipadzakhala konse mtendere mpaka Yesu Khristu adzabwere.” Ndipo ndinati, “Padzakhala timalingaliro titatu tatikulu, Chikominisi, Fascism, ndi Nazism.” Ndipo ndinati, “Izo zidzathera mu lingaliro limodzi, ndipo lingaliro limodzi limenelo lidzalamulira dziko lapansi ndipo lidzawotcha Mzinda wa Vatican.” Inu mukukumbukira ine ndikunena zimenezo zaka ndi zaka ndi zaka zapitazo. Ndipo ndendende basi mwanjira imeneyo!

⁴² Ine ndinati, “Basi isanafike nthawi imeneyo, kuti magalimoto. . .” Amene anamangidwa molunjika mwakale mmbuyo umo, zaka twente zapitazo kapena zaka twente-faivi zapitazo. Inu mukhoza kukumbukira zaka twente mulimonse. Ndipo ine ndinati, “Iwo azidzawoneka ngati dzira. Iwo adzawumbidwa. Amenewo ndi masomphenya. Adzakhala

chinachake mmawonekedwe a chinachake chonga *icho*.” Ndipo umo ndi momwe iwo ati adzakhalire Mkwatulo usanachitike.

⁴³ Koma Mulungu tsopano akumasula mpingo paliponsepo, kukonzekera tsopano kuti Iye akhoze kulowa mu Mkwatulo, ayenera kuwupatsa iwo chikhulupiriro chokwatulitsa iwo usanalowe mu Mkwatulo.

⁴⁴ Anthu ali mu mzimu wa tsiku lomaliza, monga momwe iwo anali mmasiku a Nowa, kudya, kumwa, kukwatira, kukwatiwa, zosawakhudza, osasamala, kumayendayenda, ndi china chirichonse. Ndipo anthu aku America awa ndi oyipa kwambiri padziko lapansi! Ammutu, amalingaliro apamwamba, osadzigwira, owopsya, ndi onyoza, odziwazo-zonse. Ngati alipo malo aliwonse padziko lapansi... Ndi Baibulo langa pa mtima wanga, ndipo Mulungu podziwa kuti ine... akuyang'ana pansu pa ine ndipo akudziwa kuti ine ndiyenera ndidzaima pamaso Pake mmawa usanafike. Ngati ndikanati ndinene chomwecho, malowa akusowekera amishonare moipitsitsa kuposa malo aliwonse padziko lapansi, ndi U.S.A., United States of America. Gulu lalikulu kwambiri la achikunja omwe ine ndikuwadziwa kulikonse, ali mu Amerika. *Heathen* amatanthauza “wosakhulupirira.”

⁴⁵ Oh, iwo amakhulupirira fioloje. Iwo ndi ankhanza kwambiri ndipo obwerera mmbuyo mpaka inu simungathe kuyankhula nawo mwanjira iliyonse. Ine ndikhoza kumutenga munthu kunja uko, yemwe sanamvepo za Mulungu, akupembedza fano, ndi kuchita naye zambiri mu mphindi faivi kuposa momwe mungachitire ndi munthu amene amadzinenera kuti ndi Mkristu, kamba wakale chinachake chimene chinapachikika pamenepo ndipo chinali ndi madzi ambiri owumitsira mitembo awa, ndi kukhuthukira mmitsempha yake. Zimandiyika ine mu malingaliro a imodzi ya malo osungiramo mitembo akale ozizira kumusi kuno kwinakwake, ngati malo osungiramo maliro. Uko nkulondola. Kukhala mozungulira pamenepo, kukalowa mkati, kukaika... Ine ndimapita mmatchalitchi akale, amenewo aakulu, ndipo izo zimandiyika ine mmalingaliro a—nyumba yosungiramo mitembo. Choyezera chاوزimu chimapita handiredi pansu pa ziro. Iwe umayenera kudzigwedezera wekha mkati, pafupifupi. Ine sindikunena izi mwa nthabwala, koma ndi zoon. Ena a iwo samadziwa nkomwe za Mulungu, amaimirira pamenepo ndikuti, “Chabwino, tsopano, ine ndikuuzani inu, ine ndikukhulupirira ndizo zonse...” Mai, kalanga! Bwanji, iwe wonyenga anthu, iwe ukukhala kunja kwa Ufumu wa Mulungu ndipo ukuphunzitsa ena kuti akhale kunja. Iwo amaika madzi enaake mmenemo, monga kumutengera munthu wakufa ku nyumba yosungiramo mitembo. Iwo—iwo amachotsa magazi ake onse, ndi kuikamo chinachake mmenemo kuti atsimikizire kuti iye wafa. Chabwino, umo ndi momwe iwo amachitira. Amatenga chipembedzo pang'ono chomwe anthu

ali nacho, kapena chikhulupiriro pang'ono chomwe iwo ali nacho, ndi kubayiramo zakale zina, ndi—ndi fioloje mwa iwo, ndi kuwapha iwo moyipitsitsa, ndi kuwasunga iwo akufa. Ndizo zonse. Izo nzoona. Zowopsya! Mai! Ndiyeno iwo amati, “Oh!”

Ine ndinanena kwa mkazi, “Kodi ndinu Mkhristu?”

Iye anati, “Ine ndikupatsani inu kuti mumvetsetse, kuti ndine wa Chimerika.”

Ine ndinati, “Izo sizomwe ine ndinakufunsani inu.”

Wina anabwera pa nsanja, anati, M'bale Bosworth anati, “Kodi ndinu Mkhristu, dona?”

⁴⁶ Iye anati, “Bwanji, kwambiri... Chabwino,” iye anati, “Ine ndikupatsani inu kuti mumvetsetse, ine ndimayatsa kandulo usiku uliwonse.” Oh, mai! Kuyatsa kandulo usiku uliwonse, zimakupangatsani inu kukhala Mkhristu? Iwe ukhoza kuliwotcha dziko lonse, izo sizingakuthandize iwe nkomwe. Mpaka Moto woyaka wa Mzimu Woyera utayeretsa solo yako ku tchimo, iwe ukadali wochimwa! Izo zimakhala mu mtima.

⁴⁷ “Chabwino, ine ndimakhala ku Amerika.” Chabwino, izo sizimapanga kusiyanana kulikonse. Izo sizimakupanga iwe kalikonseko. Mulungu samandilemekeza ine chifukwa ndine waku Amerika. Iye samamulemekeza wa chi German chifukwa iye ndi wa chi German, kapena—kapena wa chi Poland chifukwa iye ndi wochokera ku Poland. Iye samalemekeza wa chi Afrika chifukwa iye ndi wochokera ku Afrika. Mulungu samakhala ndi chidwi ndi Africa, komanso Iye samakhala ndi chidwi ndi Germany, kapena Iye samakhala ndi chidwi ndi United States. Mulungu amakhala ndi chidwi mu Ufumu umodzi, ndipo umenewo ndi Ufumu wa Mulungu, ndipo munthu wochokera ku mafuko onse amabwera mwa Iwo. Ndipo iwo amabadwira mwa Iwo kudzera mwa Mbewu ya Abrahamu, yomwe inali Yesu Khristu, ndipo amakhala olandira cholowa molingana ndi lonjezo.

⁴⁸ Fuko lirilonse pansu pa Kumwamba limalamuliridwa ndi Satana. Baibulo linanena chomwecho. Mnyamata, izo zimayika chinthu chotsamwitsa, sichoncho izo? Satana anamutengera Yesu Khristu pamwamba ndipo anakamuwonetsa Iye maufumu onse a dziko lapansi. Ndi kulondola uko? Ndipo iye anati, “Iwo ndi anga ndipo ine ndimachita nawo iwo zomwe ine ndikufuna. Ndipo ndiwapereka iwo kwa iwe ngati iwe ugwada pansu ndi kundipembedza ine.”

⁴⁹ Yesu anati, “Choka pano, Satana!” Mukuona? Yesu ankadziwa kuti Iye adzakhala Wolandira wa maufumu amenewo.

⁵⁰ Tsopano uko mu Chivumbulutso, pamene kutha kwa dziko, Baibulo linati, “Sangalalani, inu miyamba, ndi onse inu aneneri oyera, chifukwa cha maufumu a dziko lapansi adzakhala

maufumu a Ambuye wathu ndi Khristu Wake, ndipo Iye adzalamulira ndi kulamulira kwanthawizonse.”

⁵¹ Daniele anamuwona Iye ngati thanthwe losemedwa kuchokera pa phiri, likugudubuzikira mkati ndi kudzakantha fanolo kuphazi, ndi kuliphwanya ilo mzidutswa, ndipo Ufumu wa Mulungu unakula. Pamene Khristu adzatenga ulamuliro, mu Zakachikwi, uko sikudzakhala kuli matenda, kopanda chisoni. Aliyense, mikono yonse idza—idzapunthidwa kukhala zolimira, ndipo ife sitidzaphunziranso za nkondo aponso. Ndizo zonse. Izo zonse zidzakhala zitatha pamene Yesu adzabwera. Kufikira pamene, bola ngati Satana akulamulira mafuko, ndiye padzakhala nkondo ndi mphekesera za nkondo, kufikira Yesu adzabwere. Amen.

⁵² Mulungu, mutithandize ife! Pamene ine ndikuyang’ana pa inu ndikuzindikira usikuuno, nditaima pano ndikuphunzitsa kuchokera mu Mawu a Mulungu, kuti ndinu anthu opita Kumuyaya. Mwamuna ndi mkazi aliyense, mnyamata ndi mtsikana, muno, adzakayima mu Kukhalapo kwa Khristu tsiku lina. Ine ndidzayenera ndidzakayankhire pa zomwe ine ndinanena pamaso panu, monga wantchito Wake. Ndipo ine ndingaleke bwanji kukuwuzani inu Choonadi cha Mulungu? Ngati Mulungu walemekeza kwambiri Mawu amene ine ndawalalikira, mpaka Iye wawasesa Iwo kuzungulira dziko lapansi, ndipo wawalemekeza Iwo mnyumba zachifumu ndi kulikonseko, ndipo palibe nthawi imodzi imene Iye ananenapo kalikonse koma chimene izo zinali ndendende basi momwe Iye ananenera izo, ndiye ndithudi Iye sangandilole ine kuti ndinene chinachake chimene chinali cholakwika. Ndipo ine ndikunena usikuuno, mzanga wa Chikristu, ziribe kanthu kuti ndiwe wa mpingo wanji, kulikonse kumene iwe uli, ngati iwe siuli mu Ufumu wa Mulungu, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera kukubweretsa iwe mu Thupi la Khristu, iwe ukanikizire mkati tsopano, pakuti iwe sukudziwa ora lomwe Iye akubwera.

⁵³ Israeli kumusi uko tsopano mu Igupto, choyimira cha Mpingo ukutulutsidwa, Eksodo, mutu wa 1. Israeli anali ku Igupto, pambuyo pa Yosefe. Tsopano izo zikundipatsa ine ndendende basi pafupifupi, pafupi maminiti sarte. Ine ndiyetsa kusunghanitsa zochuluka za izo momwe ine ndingathere. Tsopano, iwo anali mu Igupto chifukwa cha chilala, Isaki akupita kumeneko, ndipo akutenga mbadwa. Ndipo kumeneko iwo ankakhala mu Gosheni. Koma Yosefe, pamene iye anafa, (kufotokoza kokongola) iye anatchula za kuchoka kwa ana a Israeli, ndipo anatchula zokhudza mafupa ake. Mvetserani. Ngati inu mungandikhulukire, ine ndikufuna ndigwetserepo. . .

⁵⁴ Inu mukudziwa, ngati mungawerenge Mawu monga *chonchi* apa, izo ziri bwino, koma inu ndithudi mukhoza kuphonya matanthauzo a Iwo. Mawu amalembedwa pakati pa mizere.

Yesu anati, “Ine ndazibisa Izo kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo ndaziululira Izo kwa makanda amene ati adzaphunzire.” Maseminare a zafioloje awa ali chimodzimodzi basi monga ansembe aja anali kumbuyo uko, ndi wansembe wamkulu ndi onse a iwo, amene ankawerenga Mawu koma analephera kuti amuwone Yesu kukhala Khristu. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

⁵⁵ Tsopano tayang’anani pa mbadwa zimenezo. Ndi chifukwa chiyani Yakobo wokalambayo, pamene iye amafa kumusi uko mu—mu Igupto anati, “Musadzandiyike ine kuno”? Ndipo iye anamupangitsa Yosefe kuyika dzanja lake pa ntchafu yolumalayo, ndipo analumbira pa Mulungu kuti sadzaika mmanda mafupa ake kumeneko. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Anati, “Mudzanditengere ine kwathu ndi kukandiyikako ine mmanda.”

⁵⁶ Tayang’anani pa Yobu kumbuyo uko atakhala, atazingwa, atasefukira ndi zithupsya, ndipo iye anatemberera tsiku limene iye anabadwa. Bukhu lakale kwambiri mu Baibulo ndi Yobu, ndipo ilo linalembedwa Genesis lisanalembedwe. Penyani iye atayima pamenepo, akupesa yake...ali ndi phale, atakhala panja kuseri, pa mulu wa phulusa. Ine ndinalalikira za zimenezo kuno nthawi ina kwa pafupifupi miyezi itatu molunjika. Anthu ena amandipatsa ine, amandilemba ine, kumandiuza ine, ankati, “M’bale Bill, ndi liti pamene inu mudzamuchotse Yobu pa mulu wa phulusa?” Ndipo ine—ine...za iye atakhala pamenepo. Nthawi yopambana ija ya kusankha, chinachake chinkayenera kuti chichitidwe. Ora la ziro lija. Koma inu mukudziwa chimene chinachitika pamene ife tinamuchotsa iye pa mulu wa phulusa, chinachake chinachitika.

⁵⁷ Umo ndi momwe ife timayesera kuchita zitsitsimutso izi. Ife timatengera chidwi cha anthu kulozera kwa Khristu, kenako nkuwagwira malo awa mpaka utapeza malo omwe ungakayendetsereko izo. Ndicho chinthucho. Ndiwo Mzimu Woyera ukukonzekera. Kumamverera Mzimu ukusuntha pakati pa anthu, ndipo umadziwa pamene kupha kwakonzeka.

⁵⁸ Zindikirani, ndi ameneyo Yobu atakhala pamenepo, wokhumudwitsidwa. Mkazi wake kumene anamutembenukira iye, nayenda nati, “Yobu, bwanji osatukwana Mulungu, ndi kufa?”

⁵⁹ Iye anati, “Iwe ukuyankhula ngati mkazi wopusa.” Iye anati, “Ambuye wapereka, Ambuye watenga, lodala likhale Dzina la Ambuye.”

⁶⁰ Apa panabwera mamembala a mpingo kumeneko ndipo anadzakhala atatembenezira misana yawo kwa iye kwa masiku seveni, ndi chithonhozo bwanji! Anati, “Yobu, ndiwe wochimwa wamseri. Iwe wakhala ukuchimwa.” Yobu ankadziwa kuti iye

anali asanachimwepo. Anawonetsa chimene iwo ankadziwa zokhudza zimenezo.

⁶¹ Chotero, mu kukhumudwako, munthu wolungama, Mulungu akuchita ndi woyera mtima, Iye anatumizako munthu dzina lake Elihu. Ndipo Elihu sanamutsutse iye; kokha kumutsutsa Mulungu. Koma Elihu anamuuzza iye, anati, “Tsopano, Yobu, iwe wawona zinthu zonse izi.” Iye anati, “Tsopano, pakubwera Mmodzi Wolungama Amene ati adzayime mu cholekanitsa pakati pa munthu wochimwa ndi Mulungu woyera. Ndiyeno adzakhala munthu ameneyo yemwe iwo ati adzapite ku manda kuti akamulire, ndipo iwe sukuzimvetisa izo, zikadzatero iye adzawuka.”

⁶² Ndiye pamene Yobu anamva zimenezo, iye anaimirira pa mapazi ake. Mai! Mphezi zinang’anima, mabingu anabangula. Chinali chiyani chimenecho? Mneneri anabwerera mu mpita wa Mulungu kachiwiri. Mai! Maso ake anatseguka. Iye anati, “Ine ndikudziwa Muwomboli wanga ali moyo.” Taonani, zaka foro sauzande Iye asanabwere pa dziko lapansi, “Ine ndikudziwa Muwomboli wanga ali moyo!” Kupitirira, “Ali moyo!” “Ndipo pa masiku otsiriza,” zaka thuu sauzande zotsiriza, “Iye adzaima pa dziko lapansi. Ngakhale mphutsi zitawononga thupi ili, komabe mu mnofu wanga ine ndidzamuwona Mulungu; Yemwe ine ndidzamuwona ndekha, ndipo maso anga adzamuwona, ndipo osati wina.” Ndi zimenezotu pamenepo. Pamene iye anakonzekera kuti afe, anati, “Mudzandiike ine cha kuno ku Palestina.”

⁶³ Kenako panadzabwera Abrahamu ndi lonjezo. Sarah anafa, iye anamuika iye pafupi ndi Yobu, anagula kagawo ka malo ndi kumuyikapo iye. Pamene Abrahamu anafa, iye anagona pafupi ndi Sarah.

Abrahamu anabala Isaki. Isaki anafa, ndipo iye anagona ndi Abrahamu.

⁶⁴ Isaki anabala Yakobo. Yakobo anafa, kumusi uko mu Igupto, iye anati, “Musadzandiyike ine kuno. Lumbirirani kuti inu simudzandiyika ine kuno! Mudzatengere mafupa anga ndipo mudzakawayike iwo kuntunda uko limodzi ndi abambo anga.” Chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani? Izo sizinalembedwe, m’bale, ziri pakati pa mzere.

⁶⁵ Yosefe, pamene iye anafa, anati, “Tsopano, inu muyike mafupa anga umu mu bokosi, koma musadzandiyike ine kuno. Musadzandiyike ine kumusi kuno. Inu mudzanditengere ine kuntunda uko ndipo mudzakandiyike ine, uko mdziko lolonjezedwa. Mudzakandiyike ine kuntunda uko.” Chifukwa chiyani? Anati, “Mulungu adzakuchezerani inu tsiku lina. Ine ndikusiya mafupa anga kuno kuti adzaimirire chinachake.”

Chimodzimodzi monga momwe Yosefe anasiyira mafupa ake, momwemonso Yesu anasiya manda otseguka!

⁶⁶ Muhebri aliyense wokalamba, amamenya pa nsana, wotopa ndi wothodwa, amadzandima cha kumeneko, ndipo Aigupto onse awo akayang'ana kumeneko ndi kuwona bokosi laling'ono lakale lija. Ine ndimayenera kuti ndiyang'ane pa izo kuno osati kale litali, kabokosi kakang'ono ka mtovu, kanthu kophwanyika. Ndiko kumene mafupa ake ayenera kuti anagona. Iwo ali nawo iwo ku nyumba yosungiramo zinthu zakale kumeneko, ndipo ine ndinayang'ana pa izo, iye anati, “Ndiko kumene mafupa a Yosefe anaikidwa pamene Mose anawanyamula iwo ndi iye.” Ndipo Muhebri aliyense akuyang'ana mmenemo, ankati, “Tsiku lina zidzasinthidwa kumusi kuno. Ife tidzatuluka.” Mneneri, iwo anali ndi chikhotho chokongola, chimene chinkaimira Khristu mwa njira iliyonse, monga ife tinali nazo mu phunziro la usiku wathawu. “Iye anati!” Chifukwa iye ankadalira pa zimene Mulungu anamuza Abrahamu. Ndi zimenezotu pamene.

⁶⁷ Ine ndikudalirabe chinthu chomwecho usikuuno, chimene Mulungu anamuza Abrahamu, “Ine ndidzakupulumutsa iwe ndi Mbewu yako.” Ine ndikukhulupirira zimenezo.

⁶⁸ “Tsikulina inu mudzachoka kuno,” ndipo iwo anakhulupirira zimenezo. Ndipo tsiku lina, mafupa a Yosefe wokalamba . . .

⁶⁹ Mose anayamba kutuluka, Mzimu Woyera unayankhula ndi iye, unati, “Inu mukuyiwala chinachake, Mose. Pitani kumusi ndipo mukatenge—mafupa a Yosefe.” Mose anawakulunga iwo, ndipo apa iye akubwera.

⁷⁰ Lawi la Moto likumutsogolera iye wa ku dziko lolonjezedwa, ndipo anakawakwirira iwo pambali pa Isaki ndi Yakobo. Chifukwa chiyani? Iwo ankadziwa kuti kunali kudza zipatso zoyamba za iwo amene anagona. Iwo ankadziwa kuti kunali kudza chiukitsiro, limodzi la masiku amenewo. Iwo ankadziwa Mmodzi Wolungamayo, yemwe Yobu anati, “Ine ndikudziwa Muwomboli wanga ali moyo, ndipo pa tsiku lotsiriza Iye adzayima pa dziko lapansi.” Ndipo iwo anadziwa kuti Yobu anali nalo lingaliro pamene Iye akanati ayime, kotero iye anati, “Mudzandiyike ine kuno.” Iwo ankafuna kudzakhala ndi Yosefe, kapena ndi Yobu, ndipo iwo anakwiriridwa cha kumeneko mu Palestina chifukwa ilo linali dziko lolonjezedwa. Ndipo iwo ankadziwa kuti chiukitsiro sichikanati chidzakhale mu Igupto, icho sichikanati chidzakhale ku Uluya, icho sichikanadzakhala kwina kulikonseko. Icho chikanadzakhala ku Palestina, kotero iwo anakawaika iwo kumeneko.

⁷¹ Kenako kunadzabwera Yesu, iwo . . . Mmodzi wolonjezedwayo. Iwo anamuchitira Iye zomwe iwo ananena kuti iwo akanadzatero, ndipo, oh, iwo anamupha Iye, Iye anafa. solo yake inatsikira ku gehena. Anakalalikira kwa miyoyo imene ili mu ndende. Anakatengako makiyi a imfa ndi gehena kumulanda mdierekezi. Anabwereranso mmawa wa Isitala.

Ndipo pamene Iye ankabwera kudutsa Paradiso, Iye anagogoda pakhomu, aleluya, ine ndikukhoza kumumva Iye akuti, “Ana!”

Abrahamu akuti, “Ndi ndani Ameneyo?”

“Ine ndine Mbewu yako, Mbewu ya Abrahamu.”

Daniele anati, “Ndi ndi Ameneyo?”

“Ndine Mwala umene unadulidwa kuchokera ku phiri.”

⁷² Ndi awo pamenepo, oyera a Chipangano Chakale atagona pamenepo, akuyembekezera kuti avekedwe, mu Paradiso. Iye anatsegula chitseko. Abrahamu anati, “Kodi ife tikutuluka?”

“Kwatsala pang’ono kuti kuche pa dziko lapansi. Tiyeni tikonzekere kuti tizipita.”

⁷³ Abrahamu anati, “Kodi tingaimoko pang’ono? Ine ndikufuna ndiwuwonenso mzindawu.”

⁷⁴ “Chabwino, inde, Ine ndikukawachezera ophunzira Anga kwa masiku forte.” Ndipo mmawa wa Isitara Iye anauka!

⁷⁵ Ndipo Mateyu 27 amanena kuti, “Matupi ambiri a oyera amene anagona mu fumbi la dziko lapansi, anawuka, ndipo anatulukira mu mzinda, ndipo anawonekera kwa ambiri a iwo mu mzindawo.”

⁷⁶ Ine ndikukhoza kumuwona Sarah ndi Abrahamu akubwera wapansi mu msewu, akuti, “Oh, wokonedwa, tawona apo! Iwo asintha zinthu izi pang’ono pokha. Tayag’ana cha apa momwe izi zikuwonekera.”

⁷⁷ Winawake anati, “Kodi banja lija ndi ndani pamenepo? Izo zikuwoneka ngati iwo ndi alendo.”

⁷⁸ Iwo akuti, “Ife atidziwa.” [M’bale Branham akukhwatichitsa chala chake—Mkonzi]. Anachoka pamaso pawo, monga Iye anadutsira pa khoma, inu mukudziwa, ndipo iwo sanamudziwe nkomwe kapena kumuwona Iye akubwera mmenemo. Anachokapo! Iwo anali ndi matupi aulemelero, ndipo iwo anawonekeranso padziko lapansi, aleluya, kwa zipatso zoyamba za umboni wa mphamvu ya Mulungu ndi chiwukitsiro. Apo iwo anali. Kuberedwa ndi kuvulidwa maulamuliro, ndipo anaitenga imfa ndi gehena, nkuzikantha izo. Ndipo anawuka mmawa wa Isitara, ndipo analowa mu Ufumu ndi Iye.

⁷⁹ Nzosadabwitsa iwo anati, “Mudzandiyike ine ku Palestina.” Iwo ankadziwa kuti chiukitsiro chikanati chidzakhale mu Palestina.

⁸⁰ Chotero, lero, m’bale, inu mukhoza kukhala nacho chirichonse chimene inu mukufuna, chipembedzo chonse chozizira chakale chamwambo chimene inu mukuchifuna, koma, mudzandiyike ine mwa Khristu, pakuti iwo amene ali mwa Khristu Mulungu adzawabweretsa limodzi ndi Iye mu chiwukitsiro. Nenani chirichonse chimene inu mukufuna, ndi kuzitcha izo kutentheka ndi chirichonse chimene inu

mukufuna kuti muchite, koma mungondilola ine ndikhale mwa Iye, pakuti iwo amene ali mwa Iye adzatuluka mmanda pa chiwukitsiro, pakuti Mulungu adzawaukitsa iwo. Iye analonjeza kuti adzachita izo. Ameni!

⁸¹ Zimapanga kusiyana kotani ngati inu mukukalamba? Chabwino, ulemelero kwa Mulungu! Kodi izo ziri ndi chochita chanji ndi zimenezo? Kuyandikira kwathu! Ameni. Oh, ulemelero! Munditcha ine woyera wodzigudubuza, mulimonse, inu mukhoza ngakhale kuyambapo. Chabwino. Ndi zodabwitsa bwanji! Izo ndi zokwanira kupanga woyera wodzigudubuza kuchokera mwa inu. Bwanji, ine ndingaleke bwanji kukhala wokondwa, ndi kudziwa kuti ndicho Choonadi? Bwanji, ndithudi, ndine wokondwa. Ndipo aliyense amene ali ndi chiyembekezo chimenecho akutumphuka.

⁸² Ine ndinkakonda kupita ku kasupe wakale kumene ine ndimakonda kukamwa. Junior, ine ndinkakonda kupita kumusi kumeneko. Ndipo ine ndinaganiza, pamene ine ndinali kulondera, ine ndinkapita ku kasupe wakale uyu. Ndipo ine ndinkati icho chinali chinthu chosangalatsa kwambiri kumusi uko, kumusi kwa Milltown. Ine ndinkakonda kuyang'ana pa izo, ndipo ine ndinkaganiza, “Chabwino, chabwino, nchiyani chimakupangitsa iwe kukhala wosangalala chomwechi?” Iwo—iwo umangotumphuka, kutumphuka, kutumphuka, kumatumphuka nthawi zonse. Madzi abwino kwambiri omwe ine ndinamwapo. Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, ndi chiyani chimakupangitsa iwe kukhala wosangalala kwambiri, chifukwa ziweto zimamwa mwa iwe?”

“Ayi, M'bale Bill, izo sindizo zomwe izo ziri.”

“Chabwino, nchiyani chimakupangitsa iwe kumatumphuka nthawi zonse? Chifukwa chakuti—chakuti winawake amabwera kuno, kudzatunga madzi?”

“Ayi, izo si ndizo.”

“Chabwino, mwinamwake iwe umangotumphuka chifukwa ine ndikumwa iwo.”

“Ayi.”

Ine ndinati, “Chabwino, iwe ukutumphukira chiyani?”

Ngati iye akanakhoza kuyankhula, iye akanati, “M'bale Bill, uyo si ine akutumphukayo. Ndi chinachake kumbuyo kwanga chikundikankha ine, kutumphuka.”

⁸³ Ndipo pamene Mzimu Woyera ubwera mwa munthu, pamakhala chinachake, kutuluka, akasupe a Madzi amene akutumphukira ku Moyo wosatha. Inu mungakhoze bwanji . . . ? Yesu anamuza mkazi wa pa chitsime, “Iye amene amwa Madzi awa adzakhala nawo Moyo wosatha. Izo zidzakhala mwa iye, akasupe a Madzi, akutumphukira ku Moyo wosatha.” Aleluya! (Tiyeni tibwerere ku Eksodo.) Oh, mai, taganizani za zimenezo!

⁸⁴ Moyo Wosatha, pambuyo pa kudutsa zaka teni sauzande milioni! Pamene nyanja zakale izi, chimene kuposa magawo awiri pa atatu a ili, madzi, a dziko lapansi ndi ophimbidwa ndi madzi, zizidzasesa kudutsa mu zothamanga zazikulu izo kunja uko, pamene izo zizidzagudubuzika kukula kawiri kapena katatu ngati kachisi uyu, kugumukira mu zombo, kugwera mbali ina, ina; ena a masiku awa, m'bale, izo zidzatero... tchimo litawunjikidwa mulu padziko lapansi mpaka iwo adzadziririra okha mu zipululu. Pamene sikudzakhalanso nyanja, sikudzakhalanso miyezi, sikudzakhalanso nyenyezi. Aleluya! Ine ndidzakhala ndikukhalabe moyo! Ndipo amuna ndi akazi ena onse obadwa mwatsopano adzakhala akukhala mu Kukhalapo Kwake kopambana, kutaliko, atapangidwa, atawumbidwa mu chifaniziro cha Mwana Wake wobadwa yekha. Mwa chisomo chake ife tinapululumutsidwa!

⁸⁵ Nzosadabwitsa wandakatulo ananena kuti, “Chikondi cha Mulungu, cholemera bwanji, choyera bwanji, chopanda chidziwitso ndi champhamvu bwanji! Ichu chidzakhaliisa kwanthawizonse, nyimbo ya oyera ndi Angelo.” Ife tingakhale bwanji chete? Mai!

“Kodi ndi umboni, M'bale Branham?” Eya.

⁸⁶ Tsopano, Isaki, Yakobo, ndipo tsopano Yosefe. Ndipo Yosefe anafa, chinali chitsanzo changwirowo bwanji chimenecho, mafupa ake anasiyidwa pamenepo ngati chikumbutso.

⁸⁷ Kuno osati kale litali... Ine sindikuganiza kuti Billy ali kumbuyo uko, ine sindimanena izi kwa iye pamene iye ali pafupi. Ife tinkayika duwa pamanda a amayi ake, Kukongoletsa m'mawa. Iye anali akulira, atayima pamenepo. Ndipo ine ndinati, “Billy, usalire. Ungotseka maso ako, uyang'ane kutsidya kwa nyanja kutaliko.” Ine ndinati, “Amayi agona kumeneko, ndipo mlongo wako wamng'ono wagona ndi iye; koma iwo siali kumeneko. Kuli manda apululu kutsidya la nyanja kutaliko.” Aleluya!

⁸⁸ Ndi kumene ine ndikuyang'anako, chimodzimidzi monga Ahebri ankawonera, “Tsiku lina ife tidzatuluka.” Ndipo tsiku lina ife tidzatuluka! Ine sindidzambanso izo za “phulusa ku phulusa, kapena fumbi ku fumbi, ndi nthaka ku nthaka,” koma chimene ine ndikuganiza, “Tsiku lina!”

⁸⁹ Tsiku lina pamene ine ndinali kulalikirira pa maliro a sheriff wakale kuno, wa mzindawu. Mnyamatayo anali atangobwera kwa Khristu, mu maora pang'ono asanafe. Ine ndinawawona abambo ake amutu waimvi akufika pa bokosilo, ndi milomo yonjenjemera ndi misozi ikutsikira pansu, anadzamupsyopsyona mnyamata ameneyo yenda-bwino, ndipo anatsala pang'ono kugwera mu bokosilo. Ine ndinamva zimenezo, ine ndinapotolokera mmbuyo. Ndipo iye anadzaika maluwapo. Anapotoloka, ndipo ine ndinati, “Phulusa ku

phulusa, ndi fumbi ku fumbi, ndi nthaka ku nthaka.” Ine ndinaganiza, “Tsiku lina laulemlero! M’bandakucha wagolide, Yesu adzabwera!” Izo nzoona. Chabwino.

⁹⁰ Kodi tifika liti ku phunzirolo? Komwe uko mu Igupto, nthawi zinali zitadutsa. (Mundipempherere ine.) Ndipo pamenepo, ndiye, apo potsiriza panadzawuka Farao yemwe sankamudziwa Yosefe. Zaka foro handiredi Mulungu analonjeza kuti iwo adzakhala kumeneko, ndipo iwo anali zaka foro handiredi ndi twente pamene iwo anadzatuluka.

⁹¹ Tsopano, mutu wa 1, kuchokera ku mutu wa 1 mpaka wa 5, ndime ya 5, ndi Israeli mu Igupto.

⁹² Ndipo kuyambira ndime ya 7, kupitirira mpaka ndime ya 22, imachita ndi usinga wawo. Ambiri a inu mwawerengapo izo nthawi zambiri, nthawi zambiri.

⁹³ Ine ndifika pa nsonga yachidule tsopano. Ine ndangotsala ndi—kanthawi pang’ono. Ndiye ife tiyambira mu mutu wa 2, kukonzekera kwa chiwombolo, kubadwa kwa Mose. Anthu anayamba kukonzekera. Ogwiritsa ntchito akumenya, ana akuphedwa. Ora la zimano za magudumu a uneneri wa Mulungu anali atafika panthawi yake.

⁹⁴ Mvetserani, ine ndikufuna kuti inu muzimvetsetse izi, ine ndikukhulupirira iwo akhazikika kwa izo kachiwiri. Ine ndikukhulupirira ife tiri pano. Ndi chifukwa chake ine ndikuganiza kuti zinthu zikuyenda momwe zikuyenderamu tsopano. Wotchi yakale yauneneri inagunda mpaka pafupifupi ora la ziro. Ndinalalikira pa zimenezo nthawi ina kale. Ndipo wojambula waku Germany anazijambula izo, ine ndiri nazo izo zitapachikidwa mu nyumba mwanga; munthu akupemphera, Baibulo litatsegulidwa, kandulo yaing’ono yamafuta ikuyaka, ndipo koloko maminiti faivi kuti ikwane thwelovu, pa chojambulidwa chamafuta. Kukonzekera, kukhala akukonzekera, Mulungu akukonzekera kuti achite chinachake. Tsopano penyani.

⁹⁵ Pamene Iye anakonzekera kuti achite chinachake, Iye anapereka kubadwa kwachirendo uko mu Igupto, kwa kamnyamata kakang’ono. Osaposa mnyamata wina aliyense. Iye anali basi mwamuna wa fuko la Levi, anapita kukadzitengera mkazi, anali Levi, ndipo iwo anali ndi mwana wamng’ono. Ndipo iwo anali kupha ana aamuna aang’ono onse, koma pamene mwana uyu anabadwa panali chinachake chodabwitsa cha mwanayo, chinachake chinachitika. Kukonzedweratu, kudzozedweratu. Mose analibe kanthu kochita ndi zimenezo. Koma iye anali Mose, koteri iwo sanawope malamulo a mfumu. Iwo anakamuyika iye mu chombo chaching’ono, ndipo iye analeredwa pansu pomwe pa khomo la Farao (kunali kulondola uko?), kuti adzakhale ngakhale mwana wake. Chabwino, tsopano.

⁹⁶ Mose, kuyambira ndime ya 11, mpaka mmusi ku ndime ya 25, ndi Mose akudzizindikiritsa yekha kwa ana a Israeli. Ambiri akudziwa momwe izo zinachitikira kumeneko. Iye anadzizindikiritsa yekha. Ndiyeno pamene iye anatero, iye ankaganiza kuti abale akanamvetsa kuti iye anali mwamunayo amene anali atatumizidwa kuti—kuti akawatulutse iwo kuchokera mu ukapolo, koma iwo analephera kuti amvetse. Ndi kulondola uko?

⁹⁷ Ndipo, oh, anthu, ndi choyimira chokongola bwanji chimenecho cha lero! Chinthu Kumene chimene chabwera kudzawombola anthu, iwo akuchiwopa Icho. Iwo akumuwopa Muwomboli.

⁹⁸ Mvetserani, pamene iwo anamanga kachisi wa Solomoni, iwo, a... Aliyense wa inu omanga pano tsopano mukhoza kuzimvetsa izi mwabwino kwambiri. Iwo amabweretsa mikunguza kumeneko kuchokera ku Lebanoni, iwo ankaiyandamitsa iyo mpaka ku Yopa, ndi kuinyamula iyo pa ngolo, ndi zina zotero, inu mukudziwa. Akatero ankadula miyala yawo yonse, konse kuzungulira dziko lapansi. Koma pamene iyo ibwera pamodzi, iyo imakhala miyala yangwiro chomwecho! Kwa zaka forte akumanga kachisi, kunalibeko phokoso la macheka kapena phokoso la nyundo. Mwala uliwonse unkapita, wina umadulidwa mwanjira *iyi*, wina umadulidwa mwanjira *iyi*, umodzi umadulidwa mmbuyo mwanjira *iyi*, koma iliyonse ya iyo imapita limodzi. Iwo anayamba kuchiyika chinthucho, kuyimanga nyumbayo, kumayenda bwino bwino. Ndipo iwo anapeza mwala-wowoneka moseketsa. Iwo sanafune chinthu chimenecho, anati, “Iwo si wa pano.” Ndipo iwo anawukankhira iwo panja, anawuonyera iwo mu mulu wa maudzu. Ndipo, anadzapeza kuti, iwo atamanga mopitirira ndi mopitirira ndi mopitirira, ndipo, anadzapeza kuti, mwala womwewo umene iwo anaukana unali mwalawapangodya waukulu. Yesu ananena chomwecho.

⁹⁹ Ndipo, lero, Amethodisti, Abaptisti, Achilutera, Achipentekoste, konsekonse kozungulira, ngati inu simusamalitsa, abwenzi; Mwalawapangodya weniweni, inu mukuwukana Iwo, ndipo Mwalawapangodya mu kumanga kwa nyumba yauzimu iyi ndi Mzimu Woyera. Inu mukuchita mantha ndi Iyo. Inu mukuchita mantha ndi kutengeka. Ine ndikudziwa ife tiri ndi zowopsyezera zakale zambiri ndi zotonza. Bwanji, ngati pakanati pasakhale izo, sipakanakhala Mmodzi weniweni. Koma pali nkhani yeniyeni ya Mzimu Woyera mu ubatizo. Izo nzoona. Chabwino. Ndipo tsopano iwo awukana Iwo, akuti, “Oh, ife sitingathe kuchita *zimenezo*. Oh, chabwino, ife sitingakhoze kukhala nawo Iwo, M’bale Branham.”

¹⁰⁰ Ine ndinanena kuno tsiku lina, pamene mphunzitsi wa koleji yayikulu anali atakhala mnyumba mwanga, ndipo kuchokera ku bungwe la Billy Graham, Dr. Sanden, gulu la iwo atakhala

pamenepo. Ndipo iwo anati, “M’bale Branham, ife tikuuzani inu limene liri vuto.” Anati, “Izo ndi zokwanira kutembenuza dziko.” Anati, “Ine ndikuwuzani limene liri vuto,” anati, “inu mumakhala ndi Achipentekoste ochuluka kwambiri ndi ojera odzigudubuzwa mu msonkhano wanu. Ndicho chimene dandaulo liri.”

Ine ndinati, “Kodi inu mungathandizire izo?”

“Chabwino, ndithudi, ife tiyenera . . .”

¹⁰¹ “Eya, ine ndimaganiza chomwecho. Ayi, inu simungatero. Ndithudi, inu simungatero.” Ndizo ndendende.

¹⁰² Mpingo ikuluikulu imeneyo ikhoza kupita patsogolo ndi kukakhala ndi fioloje yawo, ndi khwangwala wawo pa *izi* ndi kulira za *izo*, ndi kuimirira patali ndi kumayang’ana, ndi ma D.D. awo ali kumbuyo kwawo, ndi zinthu monga choncho, ndipo ena a iwo samadziwa mochulukira za Mulungu monga momwe kalulu angadziwire za kuvala nsapato za chisanu. Uko nkulondola. Oh, oh, ndithudi iwo amadziwa mawu onse Achigriki, ndipo iwo amawadziwa—maphunziro awo. Mulungu samadziwika ndi fioloje kapena maphunziro. Mulungu amadziwika ndi chikhulupiriro! Chidziwitso chimamuchotsa munthu kwa Mulungu; chikhulupiriro chimamubweretsa iye kwa Mulungu. Ndicho chimene chinamulekanitsa iye kwa Mulungu, mmunda wa Edeni, iye anapita ku mtengo wa chidziwitso.

¹⁰³ Ndipo ubatizo kumene wa Mzimu Woyera umene wabweretsa Moyo kwa anthu, chifukwa chimene Achipentekoste ndi ojera-odzigudubuzwa, monga inu mumawatchulira iwo, amandilandira ine pa phunziro la machiritso Auzimu.

¹⁰⁴ Oh, zedidi, mafumu ndi amphamvu, iwo amamva za izo, iwo amati “bwerani kuno,” Ambuye, pokhala wachifundo, amawachiritsa iwo amene ali a chonchowo. Uko nkulondola.

¹⁰⁵ Koma ena onsewo, pamene iwe uyankhula za Moyo Wamuyaya, iwo “ndi a mpingo wa Anglican,” iwo “ndi a *uwu*, *uwo*, *winawo*,” iwo “ndi a mpingo.” Izo ziribe kanthu kochita ndi zimenezo. Iwe kukhala wa mpingo sizimatanthauza *izo* ndi Mulungu, pokhapokha iwe utabadwa mwatsopano! [M’bale Branham akhwatchitsa zala zake—Mkonzi].

¹⁰⁶ Ulipo Mpingo umodzi wokha, ndipo umenewo ndi iwo amene anabadwira mu Thupi la Yesu Khristu, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Aleluya. Ndiroleni ine ndikuuzeni inu, m’bale wanga, ilipo njira imodzi yokha yolowera mwa Khristu. Imeneyo si pa kugwirana chanza, kapena ubatizo wa mmadzi, mwa kukonkha, mwa kusiya kudya nyama, mwa kusunga masiku a sabata. Pakusiya kusuta, kutafuna, kumwa, kutukwana, zinthu zonse *izi*, imeneyo sindiyo njira yolowera mwa Khristu.

107 Kusuta ndudu, kumwa kachasu, kuthamanga mozungulira ndi enawo, ndi akazi, mosaloledwa, ndi zinthu zonse izi zimene inu mumachita, izo si tchimo. Palibe kanthu. . . Izo si tchimo. Kutukwana, kulumbira, kumwa, izo si tchimo, izo ndi zikhumbo za tchimo. Ndinu wochimwa, nchiyani chimakupangitsani inu kuchita zimenezo; koma ilo si tchimo, zimenezo ndi zikhumbo zake.

108 Monga tsopano, izi zikupwetekani inu. Koma ine ndiri nawo udindo ndi Mawu a Mulungu, wololera kukambirana Iwo, nthawi iliyonse. Apa ndi pamene inu anthu Achipentekoste mwapanga kulakwitsa kwanu, ambiri a inu mwakhala pano, pa kuphunzitsa, “Umboni woyambirira wa Mzimu Woyera, kuyankhula mu malirime kukhala Mzimu Woyera.” Bwanji, kuyankhula mmalirime ndi kwabwino, koma icho ndi chikhumbo. Umenewo si Mzimu Woyera; icho ndi chimene Mzimu Woyera umachita.

109 Mzimu Woyera ndi chikondi cha Mulungu. Ine ndikhoza kutsimikizira zimenezo mwa Baibulo. “Ngakhale ine ndingayankhule ndi malirime a anthu ndi a Angelo, ndipo ndiribe chikondi, izo sizindipindulira ine kanthu.”

110 Ngati inu mukufuna mtengo wa apulo, ndipo basi mwangokhala ndi apulo, inu muli kutali kwambiri kuti muwupeze mtengowo. Mwaona, ndi chikhumbo.

111 Tchimo! Chifukwa chimene inu mumatukwana, kusuta, kumwa, kukwiya ndi kuwuluka pa chigwiriro, ndi zinthu monga zimenezo, ndi chifukwa chakuti ndinu wochimwa. Zimenezo si tchimo; ndi chifukwa chakuti ndinu wochimwa. Yesu anati, Lemba limanena izi, “Iye amene sakhulupirira waweruzidwa kale.” Ngati inu mukukhulupirira, inu simumachita zinthu zimenezo, chifukwa Moyo wa Khristu uli mwa inu. Ndipo ngati inu mumazichita zimenezo, ndi chifukwa chakuti inu ndinu wochimwa ndipo sindinu wokhulupirira. Ngakhale mutamadzinenera kuti ndi inuyo, komabe inu simuli. Mtengo umadziwika ndi zipatso zake. Tsopano, zimenezo, mulole izo zilowerere kwa miniti yokha pamene ine ndikuwerenga. Uko nkulondola. Ndizo zomwe Yesu ananena, “Mtengo umadziwika ndi zipatso zomwe iwo ukubala. Mtengo woipa subala zipatso zabwino.” Chabwino.

112 Kumusi komwe, apa iwo anabwera, nthawi ya chiwombolo. Mose anabadwa, analeredwa pa khomo la Farao, anatuluka, ndimayembekeza kuti anawo azindikira kuti iyeyo anali munthu woti achite zimenezo. Koma kodi iwo anachita zimenezo? Ayi, bwana. Iwo anati, “Ndani anakupanga iwe kukhala wolamulira wathu? Kodi iwe utipha ife monga iwe unachitira ndi wachi Igupto?” Ndipo Mose anathawa. Chabwino. Mose, wokanidwa ndi abale ake.

¹¹³ Kuyambira pa ndime ya 21 ya mutu wa 2, ife tiyimira mu miniti yokha pa izi. Ine ndikungoyesera kuti ndikupatseni inu maziko. Ife tangotsala ndi mphindi pang’ono, mwinamwake ife tidzayenera kuti tidzatsirizitse mawa usiku. Zindikirani, iye anakanidwa ndi abale ake, ndipo anapita ku dziko la Midiani ndipo anakakwatira mkazi wa Amitundu.

¹¹⁴ Choyimira changwirowo cha Khristu, chinali Mose. Ndi kulondola uko? Mbadwa zonsezo zinali Yesu Khristu akukhala moyo usanakhaleko. Mose anabadwa pansu pa chizunzo, monga momwe iwo ankaphera ana onse mu nthawi ya Mose. Yesu, pamene Iye anabwera, iwo anali akupha ana onse kuti amupeze Iye. Ndi kulondola uko? Mdierekezi kuyesetsa kuti amupeze Mose, mdierekezi kuyesetsa kuti amupeze Yesu. Iye anali akuyesetsa!

¹¹⁵ Ine ndikukhoza kumuwona Yesu pamene Iye anapita mmwamba, kumusi uko, anakagogoda pa chitseko kumusi uko mu gehena, mmawa umenewo. Aleluya! (ine sindikudziwa kaya ziri mkatimu—mwa ine kuti ndiphunzitse zimenezo panobe usikuuno.) Pamene ine ndikukhoza kumuwona Yesu pamene Iye anafa pa Kalvare, anakwera, anapita kumusi uko ndipo anakawawona anthu onse awo kumbuyo uko, akulira ndi kuisima, ndi kumapitirira, anati, “Munkayenera kuti mukawawawera aneneri.” Iye analalikira kwa miyoyo imene inali mu ndende. “Inu munali ndi Enoki, inu munali nawo aneneri, inu munali nawo malamulo, bwanji inu simunamvetsere kwa iwo?” Iwo sanatero. Chitseko chinatsekedwa.

Anapita ku gehena, anakagogoda pa chitseko. Satana anati, “Ndi ndani ali kumeneko?”

Iye anati, “Bwera, udzatsegule chitseko!” Oh, mai! Ine ndikungopereka sewero, ndithudi.

Anayenda mpaka pakhomo, ndipo anatsegula chitseko, ndipo anati, “Ndiwe ndani?”

Bwanji, Iye anati, “Ndine Yesu Khristu.”

“Oh, chotero mpaka iwe wadzafika kuno, sichoncho iwe? Huh! Ine ndakhala ndikukutsatira iwe kwa nthawi yaitali, mnyamata.”

“Ine ndikudziwa iwe watero.”

¹¹⁶ “Tsopano taonani! Ine ndinaganiza kuti ine ndinakupeza iwe pamene ine ndinapha Abele. Ine ndimaganiza kuti ine ndinakupeza iwe pamene ine ndinapha Mose. Ine ndimaganiza ine ndinakupeza iwe pamene ine ndinachita zinthu zonse izi. Pamene ndinampeza Yohane M’batizi, ndimaganiza ine ndinakupeza iwe ndithudi. Koma tsopano ine ndakupeza iwe, iwe uli kuno mmanja mwanga!”

¹¹⁷ Ine ndikukhoza kumumva Yesu Khristu akuti, “Ine ndine Mwana wa Mulungu wobadwa mwa namwali. Ine

ndinabwera kuchokera ku nyumba zachifumu za mnyanga za Atate Anga, ndipo Ine ndinabwera ku dziko lapansi. Ndipo dziko lapansi, lasambitsidwa mmawa uno ndi Magazi Anga amene Ine ndinapereka, ndipo ndalipira mtengo wa imfa, tchimo, ndi hade. Ndiipitse Ine makiyi amenewo!” Aleluya! “Ine ndikuwatenga kuyambira pano. Iwe wawasunga anthu mu ukapolo, iwe wawasunga iwo mmantha ndi china chirichonse, koma ine nditenga kuchokera apa mpakana!” Aleluya! Anawachotsapo iwo ndi kuwapachika iwo pa mbali Yake Yomwe, anamukankhira iye mmbuyo mu gehena, ndipo anachokapo. Amen. Amen!

¹¹⁸ Mgonjetsi Wamphamvu, pamene Iye anang’amba chophimba pakati, taonani, tamuonani Iye powonekera! Mgonjetsi Wamphamvu anauka, anati, “Ine ndine Iye amene ndinali wakufa, ndine wamoyo panonso, ndipo ndine wamoyo kwanthawizonse, ndipo ndiri nawo mafungulo a imfa ndi gehena.” Aleluya! “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha. Ine ndiri nawo mafungulo a chiwukitsiro, Ine ndidzamuwukitsa iye mu tsiku lotsiriza.” Izo zimandikhutitsa ine. Amen! “Ine ndine Iye.” Amen. Oh, mai!

¹¹⁹ Mose, wokanidwa ndi abale ake omwe; Yesu anakanidwa ndi abale Ake Omwe. Yosefe anakanidwa ndi abale ake omwe; kumuwona Yesu akukhala pansu kumeneko, Mzimu wa Mulungu uja ukutulukira ku Ungwiro. Ndipo apa ndi pamene Iwo unali Ungwiro, mwa Munthu uyu. Uko nkulondola. Iye anali mwa Mose, zedi Iye anali; wokanidwa ndi abale ake, ndipo anali mlendo m’dziko lake lomwe, ndipo anatenga mkazi wamitundu. Aleluya.

¹²⁰ Ana awiri, kachiwiri. Amen. Ine ndifika ku zimenezo kumapeto kwenikweni kwa maphunziro awa, kumene pafupifupi Loweruka kapena Lamlungu. Ana awiri amenewo, Efraimu ndi Manase. Ana awiri, kachiwiri. Kulondola uko?

¹²¹ Anakanidwa ndi abale ake, monga Yesu Khristu anakanidwa ndi abale Ake; anatumiza Mzimu Woyera, wokanidwa ndi abale, ndipo anabwera kuno ndipo tsopano akutenga Mkwatibwi wa Amitundu. Kupereka izo monga Yosefe; wokanidwa ndi abale ake, anatenga mkwatibwi wa Amitundu. Oh, mai! Tsopano, mutu wa 2.

¹²² Kuitana kwa Mose, chitsamba choyaka moto. Oh, ine ndikukhumba tikanakhala nayo nthawi yoti tipite mu zimenezo. Ife tiribe. Mphindi pang’ono chabe tsopano, ndiye ife tidzatero—ndiye ife tidzayesa. Pamene inu mwatopa, mukweze dzanja lanu, ndipo ine nditero—ine ndisiya, moona mtima ine nditero.

¹²³ Taonani! Oh, m’bale, izi ziri ngati buledi wa chimanga ndi nyemba, Izo zimamatira ku nthiti zako. Izi zimakugwira iwe mwanjira ina, iwe ukhoza kuchita—kuchita ntchito yabwino

ya tsiku kwa Ambuye mawa. Iwe ukhoza kutuluka panja ndi kukakumana ndi mdierekezi, ndikuti, “Ine ndikudziwa pamene ine ndaima. Osati chifukwa chakuti tsemwe linadutsa kutsikira pa nsana wanga; chifukwa cha PAKUTI ATERO AMBUYE! Chokapo, Satana, ine ndikutenga ulamuliro tsopano.”

¹²⁴ Tsopano ndife ana a Mulungu. Hmm! Liti? Tsopano! Mawa usiku? Ayi, pakali pano! Tsopano ndife ana a Mulungu! Tsopano ife tikukhala limodzi mmalo Amwambamwamba. Tsopano ndi Mzimu Woyera pano. Liti? Tsopano! Tsopano ife tiri nawo Moyo Wamuyaya. “Kodi inu mudzalowa mu Moyo Wamuyaya pamene mudzafa, M’bale Branham?” Ine ndiri nawo iwo tsopano! Ine tsopano ndiri nawo iwo. Motani? Yesu Khristu ananena chomwecho, PAKUTI ATERO AMBUYE.

Chotero, chokapo, imfa. Choka, Satana, ulibenso msinga kwa ine.

Paulo wakale! Iwo anali akumanga chipilala chophera kunja uko, anati, “Iwe ukudziwa chimene izo ziri, mnyamata? Akukadula mutu wako.”

“Ndi choncho? Ine ndamenya nkondo yabwino. Ine ndamaliza ntchitoyo. Ine ndasunga Chikhulupiriro.”

¹²⁵ “Hei! Kodi iwe unena chiyani iwe usanafe?” Imfa inati, “Ah, Myuda wamng’ono wamphuno ya ngowe iwe! Ine ndikudziwa kuti iwe unamenyedwa ndi zikwapu, ndipo anakutsitsira pansu ndi. . .zina zotero, ndipo iwo anachita *izi, izo*, kapena *zinazo*, koma tsopano ine ndakupeza iwe.” Iye anayang’ana kumeneko. Imfa inati, “Ine ndikupangitsa iwe unjenjemere ndi kukugwedeza.”

Iye anati, “Imfa, mbola yako ili kuti?”

Manda kunja uko, ndi matope (msirikali Wachiroma uja anaponya matope ena, kuti amuwunjikire iye mmenemo), anati, “Ine ndikugwira iwe.”

Anati, “O imfa iwe, mbola yako ili kuti? Manda, chigonjetso chako chiri kuti?” “Koma mathokozo akhale kwa Mulungu!”

Manda anati, “Ine ndikugwira iwe. Ine ndikuwumba iwe. Ine ndikuwumitsa iwe. Mphutsi zikudya iwe. Mafupa ako adzabwerera ku fumbi.”

¹²⁶ Koma Paulo anati, “Tayang’anani pa manda apululu amenewo kunja uko, ine ndiri mwa Iye! Aleluya! Ine ndidzawuka kachiwiri mmawa umenewo ndi kudzalandira korona amene Ambuye, Woweruza Wolungama, adzandipatse ine. Osati iwo okha, koma mmodzi aliyense wa iwo” (ngakhale iwo mu Branham Tabernacle) “amene amakonda kuwonekera Kwake.” Ameni. Ndithudi.

¹²⁷ Mdierekezi si kanthu koma chowopsyezera khwangwala, amangokuwopysezerani inu mu chinachake. Iye alibe ufulu mwalamulo nkomwe. Iye analandidwa ufulu uliwonse,

maulamuliro. Iye anawononga chirichonse pamene Iye anafa pa Kalvare. Ndi Uyu apa, akubwera chotsika tsopano.

¹²⁸ Mose anali atathawa, anali kunjira uko kuseri kwa chipululu, akuweta nkosa za Ayatero. Mai, zaka forte iye anali anali kunjira uko, ndipo iye anali nawo ana angapo. Akupita kunjira uko. Ndipo mkazi wake, wokalamba wamng'ono. . . Iye anali kanthu kakang'ono kokwiya kwambiri, ndipo Mose anali ndi kupsya mtima kwina, nayenso, kotero ine ndikuganiza iwo anali ndi nthawi yopambana uko kuseri kwa chipululu chimenecho. Sichoncho inu? Mulungu amadziwa momwe angakuwetere iwe. Inde.

¹²⁹ Kotero, mmawa wina ine ndikumuwona iye ali ndi ndodo yakale yokhotakhota, akuyenda mozungulira, akukakamirabe, usinkhu wa zaka eyite, ndi ndevu zoyera zikulendewera pansu munga *chonchi*, ndi tsitsi likulendewera pansu. Iye anayang'ana kumbali inayo, anati, "Awo ndi mawonekedwe odabwitsa." Anayang'ananso, anati, "Ndi chifukwa chiyani mtengo umenewo sukuwotcheka?" Anati, "Ine ndikukhulupirira ine ndingotembenukira kumbali."

¹³⁰ Inu mukudziwa, nthawizina iwe umamva phokoso lambiri ndipo umangotembenukira kumbali, kukawona chimene icho chiri, ndi kupulumutsidwa. Moto wochuluka, inu mukudziwa; eya, Iwo ukayamba kuyaka, Moto wa Mzimu Woyera ukayamba kuyaka, anthu amapotoloka ndipo amati, "Vuto ndi chiyani ndi zimenezo?"

¹³¹ Tsopano Mose anayamba kuyandikira, anati, "Ndikudabwa chifukwa chimene chinthu chimenecho sichikunyeka? Wakhala ukuyaka pamenepo kwa theka la ora, icho sichikunyeka panobe." Anayenda chokwera, ndipo anati, "Chabwino, ine ndingoyenda ndikawone kuti zonsezi ndi za chiyani."

¹³² Ndipo Liwu linayankhula kuchokera pamenepo, linati, "Vula nsapato zako, pamalo pamene iwe wayimapo ndi malo oyer." Tsopano, Ilo silinati, "Chotsa. . ." Ayi, Mose anati, "Ine ndivula chipewa changa." Iye anati, "Nsapato"! Chotero iye anafikira ndipo anavula nsapato zake.

Anati, "Inuyo ndinu Ndani, Ambuye?"

¹³³ Anati, "Mose!" Tsopano izi, kuyambira pa mutu wa 3, kumapita mmusi kuchokera ku ndime ya 1, mpaka pafupifupi ya 12.

Anati, Mose, Ine ndamva kubuula kwa anthu Anga, ndipo Ine ndakumbukira lonjezo Langa. (Oh, aleluya!) Ine ndikukumbukira lonjezo Langa ndi Abrahamu. Ndipo Ine ndamva kulira kwawo ndi kubuula kwawo, Ine ndatsika kuti ndiwawombole iwo. (Ameni. Ndabwera pansu kuti ndidzasunge Mawu Ake!)

¹³⁴ Ena a masiku awa, manda akale kutsidyako, miyala ya pamanda itakhala chammbali pa manda a agogo aakazi, zimenezo sizikupanga kusiyana kulikonse, “Ine ndakumbukira lonjezo Langa, Ine ndabwera pansi kuti ndidzawawombole iwo.” Ine sindikusamala, izo zibwere pakapita kanthawi, izo sizikupanga kusiyana kulikonse kwa ine. Aleluya. Ine ndikudziwa Yemwe akutsogolera sitimayo. Sichoncho inu? Ingokhalani chete.

“Ine ndabwera kudzawawombola iwo.”

“Kodi Inu muchita chiyani?”

“Mose, Ine ndikutuma iweyo.”

“O Ambuye! Kundituma ine? Ine—ine sindingakhoze kukachita zimenezo, Ambuye.”

“Oh, inde. Ine ndinakuyika iwe mdziko lino kwa cholinga chimenecho.”

¹³⁵ “Chabwino, ndine wa zaka eyite zakubadwa, ndipo wokhala ngati wowuma ku nsana wanga, ine ndikhoza kukhala ndi nyamakazi. Ndipo sindine munthu wakutha kuyankhula. Ine—ine sindingathe kuyankhula bwino.” Tsopano, Ndani anapanga kamwa ya munthu? Iye anati, “Ambuye, ngati Inu mungandiwonetse ine Ulemelero Wanu, ine ndipita.” Ameni. (Musachite mantha, mawu amenewo amatanthauza “zikhale chomwecho,” mwaona.) “Mundiwonetsere ine Ulemelero Wanu ndipo ine ndipita.” Ine ndimakonda kuwona pang’ono za Ulemelero wa Shekinah umenewo, sichoncho inu? Inde, bwana. “Ndiwonetseni ine Ulemelero Wanu, Ambuye. Tsopano, chiyani, Ulemelero Wanu ndi chiyani, Ambuye?”

“Mose, ndi chiyani icho chiri mdzanja lako?”

“Ndi ndodo, Ambuye, ndodo yakale yokhotakhota.”

¹³⁶ Anati, “Iponyere iyo pansi.” Anayiponyera iyo pansi, inasanduka njoka. Iye analumphira mmbuyo. Anati, “Igwire iyo ku mchira.” Iye anatero, iyo inasandukanso kukhala ndodo. Anati, “Tsopano, Mose, ndi chiyani icho mwa iwe. . .?” Anati, “Tenga dzanja lako, uliyike ilo pa chifuwa chako.” Iye anatero, pa mtima wake. Analitulutsa ilo, ilo linali loyera ndi khate. Onani, zikutanthauza chikumbumtima cha munthu, mtima wa munthu ndi woyera ndi khate, maganizo kumene a malingaliro ake ndi khate, tchimo. Iye analibwezeretsa ilo mu chifuwa chake, ndipo analitulutsanso ilo kachiwiri. Kodi chinayenera kuchitidwa ndi chiyani? Pamene ilo linatulukanso, ilo linali loyera, loyeretsedwa, monga ngati dzanja la khanda, monga dzanja linalo.

¹³⁷ Iye anawona ulemelero wa Mulungu. Kodi Ulemelero wa Mulungu ndi chiyani, ndiye? Zozizwitsa, zizindikiro, zodabwitsa, ndi machiritso Auzimu. “Ndiwonetsereni ine Ulemelero Wanu, Ambuye.”

¹³⁸ Pamene Iye anali atakonzeka kuti awapululumutse anthu Ake, Mose anabwerapo, Mzimu Woyera, ndi kudzasonyeza zizindikiro, zodabwitsa, ndi machiritso Auzimu. Amen. Kulondola! Kenako iye anayang'ana mdzanja lake, iye anati, "Mai!" Ndipo, penyani, iyi inali ndodo ya chiweruzo. Iyo inali ndodo, ife tipeza mu phunziro la mawa usiku za momwe ndodo iyo inagwedezekera pa Igupto. Ameneyo sanali Mo- . . . imeneyo inali ndodo ya chiweruzo cha Mulungu. Ndipo dzanja limene limagwira chiweruzo cha Mulungu liyenera kuyeretsedwa, ameni, dzanja loyeretsedwa ku khate lake. Iye ananyamula iyo, anati, "Tsopano, pita ku Igupto. M'bale wako ali panjira kumtunda kuno, ndipo iye akakhala mneneri kwa iwe, ndipo iwe ukakhala ngati Mulungu kwa iye."

¹³⁹ Apa akupita Mose, anabwerapo ndipo anati, "Yatero, ine ndiyenera ndikusiye iwe lero." Ananyamula mphongolo wakale ndi kuyikira chotchinga pa iye, monga choncho, ndipo anamuyika mkazi wake pa mphongolo wokalamba uyu, ali ndi ana pa ntchafu iliyonse, ndipo apa iye anapita. Kodi inu mungalingalire zimenezo? Bambo wachikulire, wazaka eyite zakubadwa, ndevu, ndevu zazitali ndi tsitsi lalitali, ndodo yokhotakhota mdzanja lake, kutsogoza bulu wokalamba, ndi mkazi atakhala pamenepo, ali ndi ana aamuna awiri, akupita kumeneko kukalamulira Igupto? Kodi inu mungalingalire chowoneka chonga icho?

"Akupita kumusi kuti akachite chiyani, Mose?" Ena a iwo.

¹⁴⁰ "Apa ine ndikupita." Mai, iye anali ndi nthawi yopambana. "Bwera, Zipporah." Ameneyo ndi mkazi wake, inu mukudziwa. Akukoka bulu wakaleyo, aponso, motsatira. Anati, "Tiyeni, ife tikupita ku Igupto, tikupita kumeneko kuti tikalande ulamuliro." Igupto anali ngati Russia. Zochitika zazikulu kwambiri za makina, ankhondo aakulu kwambiri mdziko, anali mu Igupto. Iye akanakhoza kusesa dziko lonse, kuseseratu mpaka pansu. Ndipo Mose anali akupita kumusi kuti akalande ulamuliro. Nkhalamba ndi ndodo mdzanja lake, mkazi atakhala pa bulu, ali ndi mwana pa ntchafu iliyonse, apa iye anali akupita, iwo anali akupita kumeneko kuti akalande ulamuliro. Chifukwa chiyani? Mulungu anali atalonjeza. Ulemelero kwa Mulungu!

¹⁴¹ Ndizo chimodzimidzi ndi pa Kadesi-barnea. Mulungu anali atawalonjeza iwo. Yoswa anati, "Ife tikhoza kuchita izo, chifukwa Mulungu ananena chomwecho!"

¹⁴² Ndi amenewotu pamenepo, akupita ku Igupto. Ndipo tsopano penyani momwe munthu angakhalire wosasamalira. Mu nyumba ya alendo, Mulungu anakumana naye iye kuno mnyumba ya alendo, ndipo akanakhoza kumupha iye, ndipo Zipporah anapita ndipo anakatenga mwala wakuthwa ndipo anawapanga mdulidwe ana ake awiri ndi mwala wakuthwa, ndipo anaponyera kachikopako pamaso pa Mose, ndipo anati,

“Ndiwe mwamuna wamagazi kwa ine,” anangopulumutsa moyo wa Mose. Kodi Mose anali kuchita chiyani? Mose analowa mu chipwirikiti cha tsiku limenelo, mpaka iye anali mu zimenezo—malo oti apiteko kumeneko, iye anayiwala chisindikizo cha mdulidwe.

¹⁴³ Ndipo ndi pamene ife tikuchita lero. Ndi pamene mipingo ya chiyeo ikulephera. Ife tiri nayo nthawi yochuluka kwambiri, Ambuye watipatsa ife ndalama zambiri, ife tikumanga matchalitchi akuluakulu, ndi misanja ikuluikulu, ndipo tikuyikamo mipando yapamwamba, ndi malimba, mpaka ife tinayiwala Chisindikizo cha Mulungu, chimene chiri ubatizo wa Mzimu Woyera. Zoono! Mulungu, titumizireni ife a—Zipporah. Uko nkulondola. Mdulidwe! Mwamuna aliyense wa ku Igputo, wa Israeli, amene sanachite mdulidwe, ankaphedwa. Ndipo mdulidwe unali chisindikizo cha lonjezo. Ndipo mdulidwe wa Chipangano Chakale, ndiwo ubatizo wa Mzimu Woyera wa Chatsopano. Ndipo munthu aliyense kunjwa kwa ubatizo wa Mzimu Woyera adzadulidwa. Ndi zimenezotu pamenepo. Mulungu, atichitire chifundo!

¹⁴⁴ Ine—ine—ine ndikudziwa kuti ndikukutopetsani, koma ine ndikungokhala ndi nthawi yoteroyo! Ine, chabwino, mwinamwake ine ndiyenera kuti ndiyime. Chabwino. Tidzangoyambira mawa usiku pa ndime ya 4 ndiye, mutu wa 4.

¹⁴⁵ Yehova, mu gawo lotsiriza la wa 4 apa, wa 3, akupanga Dzina Lake kudziwika, “INE NDINE INE INE.”

Anati, “Ine ndikati wandituma ine ndi ndani?”

Anati, “INE NDINE.”

Anati, “Anthu sakakhulupirira zimenezo.”

Anati, “Ukawauze iwo INE NDINE wakutuma iwe. INE NDINE.” Osati “Ine ndinali, ine ndidzakhala.” Koma, “INE NDINE,” ndiyo tensi yapano.

¹⁴⁶ Tsiku lina Ayuda anali atayima pamenepo akumwa madzi, ndipo akukondwera ndi kumayankhula za mana amene iwo anadya mchipululu. Ndipo Yesu anayima pakati pa anthu, Yohane Woyera 6, ndipo anafuula, mkati pa phwando. Ndipo iwo anati, “Bwanji, makolo athu anadya mana mchipululu.”

¹⁴⁷ Ndipo Iye anati, “Iwo ali, mmodzi aliyense, anafa.” Iye anati, “Koma Ine ndine Mkate wa Moyo umene umachokera kwa Mulungu Kumwamba, Mtengo wa moyo wa m’unda wa Edeni, ngati inu mukufuna. Ine ndine Mkate wa Moyo wochokera . . . kuchokera Kumwamba. Ndipo ngati munthu adya Mkate uwu ndi kumwa Magazi awa, kumwa Magazi Anga ndi kudya Mnofu Wanga, ali nawo Moyo wosatha, ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye pa tsiku lotsiriza.”

148 Iwo anati, “Munthu uyu akuchitira mwano. Kodi iye adzatipatsa bwanji ife thupi lake kuti tidye?” Iye anati, “Chabwino, tsopano, ife tikudziwa! Ife timakhulupirira Mose. Mose ndi wathu—ndi mneneri wathu. Ife timakhulupirira Mose. Ndipo makolo athu anadyetsedwa mchipunulu kwa zaka forte, ndi mana.”

149 Iye anati, “Ine ndikudziwa zimenezo.” Iye anati, “Ine ndikudziwa zimenezo. Koma mmodzi aliyense wa iwo anafa.” Iye anati, “Koma Ine ndine Mkate wa Moyo.”

“Chifukwa chiyani!” Iwo anati, “Chabwino, inu mukutanthauza kundiuza ine zimenezo?”

150 Iye anali Thanthwe limene linali mchipululu. Iye anali Mana amene anali mchipululu. Iye anali Mkatewoweyula mu kachisi. Oh, Iye anali Madzi mu Yordani. Ulemelero! Iye anali Alfa, Omega, Woyamba ndi Wotsiriza. Anali Iye Amene Anali, Amene Ali, ndi Amene Adzabwera. Iye analipo dziko lisanakhalepo, Iye adzakhalepo pamene kulibeko dziko. Muzu ndi Mphukira ya Davide, Nyenyezi ya Mmawa, Kakombo wa Mchigwa, ndi Rozi la Sharoni. Aleluya! Ziwiri zonse Muzu ndi Mphukira ya Davide, aleluya; asanakhalepo Davide, mwa Davide, ndi pambuyo pa Davide! Ulemelero! Ine ndimakhulupirira mu Umulungu wa Yesu Khristu. Iye anali woposa mneneri. Iye anali woposa munthu wabwino. Iye anali Mulungu ataphimbidwa mu thupi, Mulungu mwa Khristu, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini. Ndi Yemwe Iye anali. Ife tilowa mu zimenezo mmausiku angapo, Yemwe Iye anali. Ndi chifukwa chake inu simungakhoze kukhala nacho chikhulupiriro, chifukwa inu simukudziwa Yemwe Iye anali.

151 “Bwanji,” iwo anati, “Inu mukuti munamuwona Abrahamu, ndipo inu simunakwanitse zaka fifite.” Munthuyo sanali koma sarte. Iye anali atatopa, ndipo misonkhano Yake inali itamukokera Iye pansi. Iye anati, “Iwe sindiwe munthu wopitirira usinkhu wa zaka fifite, ndipo iwe ukuti unamuwoa Abrahamu amene wakhala wakufa zaka eyiti kapena naini handiredi?”

152 Mvetserani! Iye anati, “Abrahamu asanakhaleko, INE NDINE.” Aleluya! “Ine ndine Yehova.” Iye ndi Yehova-manase. Iye ndi Yehova-rapha! Iye ndi, Ye-... Oh, Iye... Maina onse achiwombola a Yehova anali mwa Iye, ndipo mwa Iye mukukhala chidzalo cha Umulungu mthupi; ndi Uyo pamenezo.

153 “Ine ndabwera kudzawawombola iwo. Ine ndikulengeza Dzina Langa. Uwawuze iwo kuti icho chidzakhala chikumbutso ku mibadwo yonse, kuti INE NDINE AMENE NDIRI. Osati ‘Ine ndinali’ kapena ‘Ine ndidzakhala.’ INE NDINE!”

Mulungu yemweyo anali kumeneko usiku uja ali pano usikuuno!

¹⁵⁴ “Tsopano, Ine ndikupita patsogolo pako, Ine ndidzatumiza Mngelo Wanga, ndipo Iye adzakhala mu Lawi la Moto. Ndipo Ine ndikumtumiza Iye patsogolo pako tsopano, ngati Lawi la Moto, ndipo Iye adzakutsogolera iwe.” Lawi la Moto! Lalikulu *kwambiri*, ngati mzati. “Lawi la Moto lidzapita patsogolo pako, kuti likutsogolere iwe. INE NDINE adzakhala mu Lawi la Moto limenelo.”

¹⁵⁵ Tsopano kwa Branham Tabernacle, ndi kwa inu amene muli oyanjana nawo ndipo mukudziwa zoonadi izi, kodi inu mukudziwa kuti Lawi la Moto lomwelo liri ndi ife usikuuno? Inu mukukumbukira nditajambulitsa chithunzi Chake kutsidya uko, ndipo momwe Icho chasesera padziko lapansi lonse tsopano, Lawi la Moto lomwelo limene linkamutsatira Mose kumbuyo uko mu chitsamba chonyeka. Ndi chiyani chimenecho? Sikolala aliyense pano sangayerekeze... Ngati ine ndakhala ndikupendekera apa ndi mawu awa ndi zinthu, ine ndikudziwa pamene ine ndayima. Ine ndikuganiza bwino bwino, ine ndikukhulupirira, mwa Mzimu Woyera. Ndiroleni ine ndikuuzeni inu, sikolala aliyense pano akudziwa kuti Mngelo uja Amene ankatsatira ana a Israeli kudutsa mchipululu anali Mngelo wa Pangano, ndipo Mngelo wa Pangano anali Yesu Khristu. Mose anachiyesa chuma cha Khristu kuti ndi chuma chachikulu kuposa dziko lonse la Igupto. Ndi kulondola uko? Ndithudi, Mngelo wa Pangano! Ndiye ndi chiyani Icho chiri pano ndi ife? Iwo akhoza kunena kuti ife, tachita misala, ife ndife *ichi, icho*, kapena *chinacho*, gulu la oyera odzigudubuzwa, kapena chinachake, mwinamwake iwo akhoza kunena zimenezo. Koma Mulungu Mwiniwake wadzitsimikizira Yekha mu Lawi la Moto lomwelo limene linatsogolera ana a Israeli, likutitsogolera ife mpaka lero. Aleluya! Ulemelero kwa Mulungu! Mmodzi yemweyo Uyo anali ndi Yesu Khristu mmbuyo kutaliko pamene Iye anayima ndipo Iye ananena kwa Afarisi amenewo, iwo anali atayima pamenepo, anamuza mkazi pa chitsime pamene machimo ake obisika anali, ndi zina zotero, Akugwira ntchito pakati pathu tsopano. “Iye amene Anali, Amene Alipo, ndipo Iyeyo Adzabwera!” Aleluya! Ine ndikumuyembekezera Iye, sichoncho inu? Ulemelero kwa Mulungu! Aleluya! Kupeka konse kwapita. Oh, mai!

¹⁵⁶ Pamene ine ndiyang’anitsitsa mtanda wodabwitsa pomwe Kalonga wa Ulemelero anafera, kutchuka kwanga konse ndimakuwerengera kuti ndi chabe, wosauka wausiwa... .

¹⁵⁷ Oh, mzanga wochimwa, iwe ungakhoze bwanji kuyima ndi kuwuwona mpingo wawukulu uja kutali mmithunzi yake, ukuwunjikana, ndi Lawi la Moto lija kuti liwatsogolere iwo, ndipo nkuyang’ana kumbuyo komwe kuno lero! Ndi angati ali nacho chithunzicho? Tiwone dzanja lanu. Ndi angati akufuna atakhala nacho chithunzicho? Tiyeni tiwone manja anu akukwera mmwamba. Ine ndidzakhala nazo izo mawa usiku,

pano kuti ndidzakuwonetseni inu. Chabwino. Ndi izo pamenepo, kutsimikiziridwa!

¹⁵⁸ Anthu sarte sauzande, otsutsa atayima pamenepo. Ine ndinati, “Ine sindikunena kuti ndine mchiritsi. Inu mukudziwa ine sindikutero. Ine ndimangoyankhula za Choonadi. Pamene ndinkabadwa mkanyumba kakang’ono ku Kentucky kumtunda uko, Mngelo wa Ambuye anabwera pa zenera ndipo anadzayima pamenepo, apo panali Lawi la Moto.” Ndipo ine ndinati, “Mulungu watsimikizira zimenezo. Ndipo ngati ndimanena Choonadi, Mulungu adzachitsimikizira Choonadi. Ndipo ngati ndiri wabodza, Mulungu sadzakhala ndi chochita ndi ine.” Ndipo pafupifupi nthawi imeneyo, panamveka Psyii! Apa Iye anabwera. Bungwe la American Photographer, onse awo pamenepo, *Look, Life, Times, Collier*, ndi onse amenewo. Bungwe la American Photographer linajambula chithunzi cha Ilo. Anati, “Ine ndikukhulupirira kuti ndi kuwenga maganizo. Ife tinaliwonapo Ilo kale, koma ine ndikukhulupirira...” Ndipo iwo anazitengera izo kwawo. Ndipo, pamenepo, Kuwala kunakhudza galasi. Iwo anazitengera izo kwa George J. Lacy, iwo anakaziyika izo pa chirichonse chimene iwo akanatha. Ndipo tsopano icho chinapachikidwa mu Washington, DC, mu holo ya zotchuka. Aleluya! Ndi chiyani chimenecho? Yesu Khristu ndi gulu ilo limene iwo amawatcha oyera odzigudubuzwa. Mulungu adalitse mtima wanu.

¹⁵⁹ Chithunzi chotchuka chirichonse chimene chinayamba chajambulidwapo, poyamba chimayenera kudutsa mu holo ya otsutsa. Munthu yemwe anajambula Mgonero Wotsiriza kumeneko, icho chinadutsa mu holo ya otsutsa. Bwanji, iwo anatsutsa. Izo zinamutengera iye moyo wake wonse, koma tsopano icho chinapachikidwa mu holo ya otchuka. Icho chiyenera kudutsa mu holo ya otsutsa.

¹⁶⁰ Ndipo, m’bale, mlongo, pamene ife tinayamba mu ichi chimene iwo amachitcha ichi chipembedzo cha Mzimu Woyera, kale mmbuyo zaka zapitazo, ife tinkalowa mmakola akale aang’ono, m’nyumba ya winawake, kasitolo kakang’ono kakutsogolo kwinakwake. Ndipo iwo ankayima panja, ochimwa, ankatafuna chingamu, akuseka ndi kumaseleula, ankatitcha ife oyera odzigudubuzwa. Ndi kumagona mu ndende ndi china chirichonse. Izo nzoonza. Iwo amamenyedwa, iwo ankapangidwa chipongwe.

¹⁶¹ Mlaliki wamng’ono wachikulire anakhala mnyumba mwanga tsiku lina, yemwe iwo anamuthamangitsira iye kunja kwa mzinda, ndipo iye ndi mkazi wake. Kuti adyetse ana ake. . . Iwo ankagona pa mabulangete amenewo, mabulangete onyowa, ndipo ankawapachika iwo mmwamba mmitengo ndi kuwasiya iwo awume kuyambira mmawa. Ndiye iwo ankatsikira nkamnjira ka njanji, kukatola chimanga pa nthawiyo. Anali ndi kachiwaya kokazingira kakang’ono kakale, iwo anakakonza izo

ndi mwala, ndipo iwo ankakhala moyo kwa masiku thwelovu kapena fortini pa nthawi, akadya mphale.

¹⁶² Manenjala wanga wakale, Mulungu adalitse mtima wake, M'bale Bosworth wachikulire, akugona uko ku Durban, Afrika, usikuuno, akundipempherera ine kuti ndibwere kumeneko. Anagona kutali ku Texas, ndi nsana wake utamenyedwa ndi zikwapu, pamene iwo anamuwopsyeza kuti amudula mmero wake, ndi china chirichonse. Pamene iye ankayenda ndi dzanja lothyoka, akuyesetsa kuti anyamule sutikesi yake. Atamenyedwa, chifukwa cholalikira ubatizo wa Mzimu Woyera.

¹⁶³ “Ankayendayenda atavala zikopa za nkhusa ndi zikopa za mbuzi, ndipo aumphawi, ndi mmalo a chipululu; amene dziko lapansi si oyenera kuti liwalandire.”

¹⁶⁴ Matchalitchi akuluakulu ankaseka ndi kumaloza zala zawo. Iwo ankati ife tinali oyera-odzigudubuza. Pamene ine ndinkamanga. . . ndinaika mwalawapangodya pamenepo, iwo anati iwo adzasandutsa kanthu kakang'ono kakale kameneko kukhala garaja. Zakhala ziri zaka twente zapitazo, ndipo Mzimu Woyera ukukhalabe pano. Aleluya! Ndiko kulondola. Ndipo, chimene iwo ankati chinali zotentheka ndi chirichonse, mafumu ndi maufumu kudutsa dziko lapansi achitcha! Anthu otchuka achiritsidwapo, mphamvu za Mulungu zasesa dziko lonse, mpaka pano ife tikuyima mamillioni amphamvu. Aleluya! Ndipo limodzi la mmawa uwu. . . Icho chadutsa mwa otsutsa, iwo ankati icho chidzawotchedwa. Iwo ananena kwa ine kumusi kuno, anati, “Oh, Billy, iwe wasokonezeka ubongo wako. Ndizo zonse zomwe ziripo kwa izo.” Ngakhale apongozi anga omwe anati, “Bwanji, mnyamatayo wapenga.” Koma, ngati ine ndatero, ine ndikukhala ndi nthawi yopambana.

¹⁶⁵ Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, m'bale. Mvetserani izi, ndipo ine ndikunena izi mwaulemu. Aleluya! Gehena yense siyingayimitse Izo. Izo zinadzozedwa ndi Yesu Khristu kuti zidzakhale chomwecho, ndipo izo zidzakhala. “Pakuti pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzaulaka Iwo.” Motani, ndi chiyani icho, Mpingo wa mtundu wanji? “Thupi ndi mwazi sizinaululire izi kwa iwe, Petro. Koma Atate Anga omwe ali Kumwamba awululira izo kwa iwe, vumbulutso lauzimu mwa Mzimu Woyera, la Mawu a Mulungu. Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzakhoza kuwulaka Iwo.” Iwo ukupitirira patsogolo.

¹⁶⁶ Tsopano, m'bale, pokhala kuti iye akusekedwa ndi kuzunzidwa, ndi kukankhidwira mmbuyo ndi chirichonse, umodzi wa mmawa waulemelo uwu, aleluya, Mbuye Wamkulu Amene wayima mu Ulemelo akulozera antchito Ake. . . “Osati mwa mphamvu, osati mwa nkondo, koma mwa Mzimu Wanga,” atero Ambuye. Osati mwa fioloje, ndipo osati mwa galamala,

osati mwa zinthu zina izi; koma mwa chikhulupiriro chophweka, choyera, chosaipitsidwa mwa Mwana wa Mulungu ndi chimene Iye ananena mu Mawu Ake. Iye akujambula chithunzicho. Iye akujambula chithunzi. Ndi chiyani chimenecho? Mpingo wodzazidwa ndi Mzimu Woyera umene Iye anawudzozeratu, chisanafike chiyambi cha dziko lapansi, kuti udzawonekere kutsidya mu Ulemelero Wake. Ndipo ena a mmawa awa Iye adzasesa pansu kudutsa, kuchokera Kumwamba, aleluya, munga maginito aakulu Iye adzawunyamula Mpingo wawung'ono umenewo umene wakhala ukuzunzidwa, kukawupachika Iwo kutsidya mu Holo ya Zotchuka, pamene Iwo uzidzapita kudutsa mu mlengalenga, akufuula, “Mwinjiro uwu wa mnofu ine ndidzaugwetsa, ndipo ndidzauka ndi kukatenga mphotho yosatha. Ndikufuula pamene ndizidzadutsa mu mlengalenga, Tsalani bwino! Tsalani bwino! Ora lokoma la pemphero!” Amen!

¹⁶⁷ Atate Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu usikuuno. Sindikudziwa lomwe liri vuto, basi sindinathe kulowa mu phunziro ili, mwanjira ina. Mzimu Woyera ukusuntha, ukusefukira, kusunthira kumeneko. Oh, ife tikukuthokozani Inu, tikukuthokozani Inu kuchokera mu kuya kwa mtima wathu, chifukwa cha chikondi Chanu ndi mphamvu. Zikomo Inu, Ambuye, zikomo Inu chifukwa cha anthu odzichepetsa amene...mu m'badwo wawukulu wa mdima uwu pansu apa. Mu nthawi yopambana iyi ya odzikhutitsa okha, oh, odzikuza, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa koposa kukonda Mulungu, Mzimu ukuyankhula momveka kuti mu nthawi zotsiriza zinthu izi zidzachitika. Timoteo Wachiwiri 3, mu Mawu Anu, munati iwo adzakhala “Ammutu, amalingaliro apamwamba,” kudziwa zambiri kuposa wina aliyense, “amalingaliro apamwamba, osadzigwira, aukali, ndi onyoza iwo amene ali abwino, okhala nawo mawonekedwe a umulungu, koma kumakana mphamvu yake; kwa oterowo chokaniko.”

¹⁶⁸ Mulungu, Inu munayankhula mu tsiku limenelo kuti Inu mudzakhala nawo Mpingo wawung'ono, munati, “Musawope, kagulu ka nkosa, ndi chifuniro cha Atate wanu kukupatsani inu Ufumu.”

¹⁶⁹ Zikomo Inu, Ambuye, chifukwa chotsegula maso anga osawuka, ine, wosauka wakhungu wakhungu kunjira uko mu tchimo, wobadwa m'banja lochimwa, ndipo ndinakulira pamwamba pa mbiya ya kachasu. Oh, koma, Mulungu, momwe Inu munatetezera ndi kuthandiza, ndi kudalitsa ndi kukhutitsa! Kodi ine ndingakhoze bwanji kufotokoza kumverera kwanga kwa Inu, Ambuye? O Mulungu, mulole ichi chikhale chiyambi chabe, Ambuye, kuti ine ndikhoze kupitanso ku ngodya za dziko lapansi, kulikonseko, kukalalikira Uthenga wa chiwombolo ndi chipulumutso.

¹⁷⁰ Mulungu, ugwezezeni mpingo wawung'ono wakale uwu kuposa kale lonse. Mulole Mzimu Woyera umugwire munthu aliyense pano, uwapangitse iwo kusala ndi kupemphera, ndi kugona chafufumimba usana ndi usiku, akufuula mokweza, Ambuye, mpaka chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale chiyambike apa, Ambuye, ndi kudzasesaponsepa kudutsa apa ndi kutumizamo nthawi-yachikale yomwe iti iwabweretse amuna ndi akazi kubwerera kwa Mulungu. Perekani izi, Atate, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni. Ameni.

Ife tingayime.

Oh, ndikufuna kumuwona Iye, kuyang'ana pa nkhope Yake,
Kumeneko kuyimba kosatha za chisomo Chake chopulumutsa;
Pa misewu ya Ulemelero ndilole ndikweze mawu anga;
Zonse zatha, ndiri kwathu, mosangalalabe.

¹⁷¹ Aleluya! Ine ndikuyang'ana pansa cha apa, ine ndikukumbukira bambo wachikulire amene anakonda kukhala pamenepo pamene ine ndimakhala ndikulalikira Mauthenga amenewo, akulira, akupukuta misonzi mmaso mwake, ndi kudzayika manja ake mondikumbatira ine. Tsiku lina lowala ndidzapita ndipo ndidzakamuwona iye! Ine ndikayang'ana cha kumeneko ndipo ndimamuwona wina yemwe wakhala kutsidyako, ndi Mlongo Weber wachikulire. Ine ndikuwakumbukira osiyanasiyana amenewo. Ndi Mlongo Snelling yemwe anakonda kuyimba mu kwaya, M'bale George wamng'ono wamutu wofiira amakhala kumbuyo uko, kodi iwo ali kuti? Aleluya! Iwo akutengedwera kutali mu zifuwa, aleluya, kusindikizidwira mu Ufumu wa Mulungu. Ine ndinawawona iwo pamene iwo ankapita.

¹⁷² Ine ndinamuwona M'bale George wamng'ono akupita kumeneko, iye anali akungoyang'ana kudzera pakhomo ndipo akupita wefu, wefu, ndipo anati "Ali kuti...? Chikuchitika ndi chiyani?" (Ndamupempherera mdzukululu wake wamng'ono usikuuno, iye amadwala.) Ndiyeno iye amakhoza kuyang'ana pansa pamenepo, ndipo amapitirira...Iwo anati, "Iye akumuyang'anira M'bale Bill."

¹⁷³ Iye sanali kundiyang'ana ine. Chinthu choyamba inu mukudziwa iye anatembenuzira mutu wake Kummawa, iye anati, "O Yesu, ine ndimadziwa Inu mudzabwera kudzanditenga ine!" Anatambasula manja ake ndipo anafa, anapita kukakumana ndi Mulungu. Aleluya! Oh, mai! Tiyeni tizipita Kwathu! Inu mukumukonda Iye?

¹⁷⁴ Ine ndikudabwa ngati muli mwamuna kapena mkazi muno, angati, "Ine ndikufuna ndimudziwe Iye mu chidzalo cha mphamvu Yake ya chiwukitsiro Chake," kwezani dzanja lanu.

Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Inu mukudabwa chifukwa chimene ine ndikuyembekezera kuitanira paguwa uku? Ine ndiri ndi chifukwa cha zimenezo. Chabwino, kwezani dzanja lanu. “Ine ndikufuna ndimudziwe Iye mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake.”

¹⁷⁵ Mphamvu yowukitsidwa, m’bale, ine sindikutanthauza chinachake chimene inu muyenera kukumba ndi kukoka ndi kuyesa. Ine ndikutanthauza mungodzimasula nokha ndipo Mulungu wakukwatulirani inu kutaliko, kwina kwake, kumene ndi chisangalalo basi kumukhalira moyo Iye. Palibe kanthu mu. . . Bwanji, zinthu zinazo ndi zakufa basi monga—monga thwelovu koloko, mwaona. Palibe, opanda chikhumbo nkomwe, opanda kutsutsika kwa iwo omwe ali mwa Khristu Yesu. Mai! Zinthu zakale zimenezo za mdziko, inu simukusowa kuti muzisiye izo, inu musatero; palibe choti musiyeye, izo zimangokusiyani inu. Inu, izo basi mophweka palibepo pamenepo, izo basi zimangopita kutali. Amen. Ndi angati omwe amawakonda Ambuye, nenani “Ameni.” [Osonkhana akutero “Ameni.”—Mkonzi]. Munene izo mokweza kwenikweni. “Ameni!” Chabwino.

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana. . .

Tembenukani ndipo mugwirane chanza tsopano.

. . . ndi wa tsoka;

¹⁷⁶ Gwiranani chanza ndi munthu winawake pafupi ndi inu, nenani, “Ndine wokondwa kukumana ndi inu muno mu kachisi,” ndiye zikonzeni kachiwiri.

. . . inu,
Litenge Ilo kulikonse upita.
Dzina lofunika, O ndi lokoma bwanji!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba;
Dzina lofunika, O ndi lokoma bwanji!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba.

Tsopano mwakachetechete kwenikweni, mvetserani:

Pa Dzina la Yesu kugwada,
Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
Mfumu ya mafumu Kumwamba ife
tidzamuveka Iye korona,
Pamene ulendo wathu udzatha.

Dzina lofunika, (Dzina Lofunika!) O ndi
lokoma bwanji!

¹⁷⁷ Kodi Ilo si lokoma? Chirichonse Kumwamba chinalitcha Ilo, chirichonse pa dziko lapansi chinalitcha Ilo: “Yesu.”

. . . Kumwamba;
 Dzina lofunika, (Dzina Lofunika!) O ndi
 lokoma bwanji!
 Chiyembekezo cha dziko lapansi ndi
 chisangalalo cha Kumwamba.

Tsopano ife tiweramitse mitu yathu.

¹⁷⁸ Mphunzitsi Wamkulu, Yemwe anakhala pa phiri tsiku lina, ndipo Inu munati, “Muzipemphera monga chomwechi”:


Atate athu Amene muli Kumwamba, Dzina lanu Liyeretsedwe.

Ufumu Wanu udze. Kufuna kwanu kuchitidwe, monga Kumwamba chomwechonso pansipano.

Mutipatse ife lero chakudya chathu cha lero. Ndipo mutikhululukire ife zolakwa zathu, monga ife tawakhulukira iwo amene atilakwira ife.

Ndipo musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse ife kwa woyipayo. Pakuti Wanu ndi Ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemelero, kwanthawizonse. Ameni.

Usiku wabwino. Ambuye akudalitseni inu.

Pa Dzina la Yesu . . . 

53-0326 Israeli Ndi Mpingo #2
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org